# *Kutsimikizira Kwa Kutumidwa*

Mukhoza kukhala pansi. Ndizo, ine ndinatengeka kwambiri, ndi kumvetsera ku umboni, mpaka ine ndinaiwala kutembenukira ku gulu. Wokondwa kwambiri kukhala pano usikuuno mu utumiki wa Ambuye, kukumana ndi M'bale O'Donnell. Ndipo ndimayang'ana pa ichi, kupereka zizindikiro zimenezo kwa ogontha ndi osayankhula.

2 Ndipo m'baleyo amandiuza ine, donayo usiku wina yemwe anali mu chikuku, amene anali ndi khansa yayikulu pa iye, iyo monga *choncho*, kuti iye anachiritsidwa mozizwitsa kwambiri mpaka iye anachoka pa chikuku, khansa yapita, ndipo akumangokhala ndi nthawi yopambana. Ndipo ine ndinali wothokoza kwambiri chifukwa cha zimenezo.

3 Nkwabwino kukhala pano usikuuno, M'bale O'Donnell, ndi kwa osonkhana abwino awa a anthu. Kumtunda kuno ku. . .

4 Kodi uyu ndi Tempe kapena Mesa? [M'bale akuti, "Tempe."—Mkonzi]. Tempe. Tempe. Ndipo tsopano iye yense wakula, kwambiri, kuzungulira kuno, kuyambira pamene ine ndinali mdziko lino, pafupifupi zaka sarte-faivi zapitazo, mpaka ine sindikuwadziwanso nkomwe malowa.

5 Ndipo nzabwino kwenikweni kukhala mnyumba ya Ambuye. Pamene ine ndimalowa, a—mtsikana wamng'ono anayima pamenepo, amene ali Abiti O'Donnell wamng'ono, ndi—ndi wamng'ono. . .atsikana awiri ena aang'ono, ndipo amayankhula kwa ine pa khomopo. Ndipo—ndipo ine ndinati, "Iwo amandiwuza ine kuti kuzizira usikuuno kuno." Ine ndinati, "Inu akummwera mumatsala pang'ono kuzizidwa kumusi kuno." Kotero ndiye dona wina wamng'onoyo anayang'ana pa mzakeyo, anati, chabwino, iye anali wochokera ku Iowa, ndipo winayo anati iye anali wochokera ku Minnesota. Ndipo ine ndinati. . .

6 Zimenezo zisanachitike, ine ndinati, "Pamene ine ndimachoka kunyumba kunali fortini pansi pa ziro." Mtsikana wamng'ono uyu wochokera ku Iowa, kapena Minnesota, mmodziyo, anati, chabwino, kunali fifite-thuu pansi pake pamene iye amachokako. Ndinadzapeza kuti, ine ndinali wakummwera. Fifite-thuu pansi. Ife titakhala ndi nyengo imeneyo mdziko langa, ndithudi ife tingawumeko. Fifite-thuu pansi, ndiko kuzizira kwenikweni, sichoncho iko, kumazizira chomwecho?

7 Tsopano, ife tikuwutenga uwu kukhala mwayi waukulu kudzakhala pano ndi inu, usikuuno, nthawi ino ya chiyanjano usanachitike msonkhano waukulu wa Amuna Amalonda. Ndizo, msonkhano waukuluwo udzayamba Lachinayi likubwerali, kumusi ku Ramada. Iwo udzakhala ku East Van Buren Street. Ndipo ndithudi tikukuitanirani inu nonse kumusiko. Kudzakhala oyankhula ena opambana mu msonkhano waukuluwo. Ndipo M'bale Velmer Gardner ndi mmodzi amene ine ndikumudziwa, ndiyeno ine ndikuganiza iwo ali ndi ena a amuna azamalonda amene ati adzayankhule. Ndipo ine—ine ndikukhulupirira kuti Jim Brown anali mmodzi wa iwo, ndi Dr. Reed, ndipo, ndithudi, M'bale Rose nthawizonse amakhala ali kumeneko, M'bale Osteen wochokera ku Texas.

8 Ndipo kotero ine ndikutsimikiza kuti inu mudzakhala ndi nthawi yopambana pobwera kumusi kumeneko. Ndife okondwa kwenikweni, poyembekezera msonkhano uwu. Ndikudalira kuti iwo udzakhala monga momwe unakhalira nthawi ina, koma wopambana kwambiri. Ndipo kumbukirani, iwo ndi bwerani mmodzi, bwerani nonse. Aliyense ndi woyitanidwa.

9 Ndiyeno, ngati icho chiti chikhale chifuniro cha Ambuye, ine ndikuganiza kuti ndiri ndi nthawi pang'ono yayikidwa pambali imene iwo ati adzandilole ine kuti ndidzayesere kuyankhula kachiwiri pa—pa kadzutsa wa Loweruka mmawa, ine ndikuganiza, ndi pa msonkhano wa Lamlungu masana, ndizo, ngati Ambuye alola. Ndipo chotero ine ndikuwutenga umenewo kukhala mwayi wawukulu, kuti ndidzayime ndi amuna aakulu amenewo ndi—ndi kudzapereka umboni kwa Ambuye, wa Ambuye, kani.

10 Ndipo ine ndikupemphera kuti Mulungu amudalitse M'bale O'Donnell kuno, ndi gulu labwino ili la Akhristu pano, amene akudzayenda, akuyembekezera pa Ambuye. Pakuti, moonadi, ndife amwendamnjira. Ndife amwendamnjira ndi alendo. Kuno si kwathu. "Koma ife tikufunafuna Mzinda umene Wowumanga wake ndi Wowupanga ndi Mulungu." Ndipo ife tangokhala amwendamnjira. Ife sitiri . . . Kuno si kwathu. Ife tikungodutsa m'njira iyi. Ndipo izo zikupereka mwayi wawukulu chotero.

11 Mwinamwake ngati ine ndingayike iyi mbali *iyi*, m'bale. [M'bale Branham akusintha maikrofoni—Mkonzi]. Izo zimapereka mwayi woterowo. Kodi izo ziri bwino? Uh-huh.

12 Mwayi wawukulu chotero kudzakhala pano, kudzayika mu nthawi ino ya chiyanjano ndi inu Akhristu odabwitsa. Ndipo pamene ine ndinamva kuti ine ndinali nditapatsidwa mwayi wa anthu osiyanasiyana awa, mipingo imeneyo imene inali, imandilola ine kuti ndiyankhule mwa iyo, basi msonkhano wawukuluwo usanachitike, ine ndinaganiza, "Ndi nthawi yopambana yoti tifotokoze kuyamikira kwathu momwe mabungwe osiyanasiyana awa agwirizanirana mu nthawi

zakale, mmautumiki anga kuzungulira dziko lapansi; a Assemblies of God, a Foursquare, a Dzina la Yesu, Mpingo wa Mulungu, ndi ambiri, ndi oyima pawokha kuzungulira dziko, onsewo kubwera mkati ngati mmodzi, ndi kwa ulemelero wa Mulungu." Ndipo Mulungu wakhala akuchita zinthu zina zazikulu pakati pawo, ndipo ndife oyamikira. Ndiyeno kudzabwerera kumene tingadzafotokoze athu—malingaliro athu ndi chiyanjano chathu.

13 Ndipo pamene ine ndimabwereza usiku watha, cha kuno mu Fellowship Tabernacle kumene ife tinali ndi msonkhano; ndipo ndinali ndi mzanga wachikulire, M'bale Bosworth. Ambiri a inu mukumukumbukira M'bale Bosworth. Ndipo iye ankakonda kundiwuza ine, iye ankati, "M'bale Branham, inu mukudziwa chimene chiyanjano chiri?"

Ine ndinati, "Ine ndikuganiza choncho, M'bale Bosworth."

14 Anati, "Ndi anthu awiri mu ngalawa imodzi." Chotero, inde, iye anali ndi khalidwe loseketsa. Ndipo nthawizonse ndinkazikonda zimenezo, "Abwenzi awiri mu ngalawa imodzi." Chotero, nthawizonse, bulangetilo limakokedwa pang'ono kuti limuthandize munthu winayo, inu mukudziwa, ndipo izo ndi zabwino kwambiri.

15 Tsopano, ine ndithudi ndikudalira kuti inu mundipempherera ine. Ndipo ine, lero, ine ndinamutuma mwana wanga wamwamuna kanthawi kapitako kuti akawone ngati panali aliyense amene amafuna kuti apempherer edwe. Ine kwenikweni sindinabwere kuti ndidzakhale ndi misonkhano ya machiritso, basi kuti, oh, kuti ndidzayankhule. Aliyense akudziwa kuti ine si mlaliki, amene anayamba wandimvapo ine. Koma ine ndiribe maphunziro, ndipo ine sindimatha kulalikira. Koma ine—ine kawirikawiri ndimapempherera odwala. Ndipo—ndipo pobwera, kawirikawiri anthu amasonkhana kuti apemphereredwe. Ndithudi, pali anthu odwala ambiri. Koma Lamlungu ine sindinatchule kanthu za izo, chifukwa ine ndikanawayitana anthu kuchokera ku mipingo ina, kuti adzabwere ku mipingo ina iyi imene ine ndimayenera kukakhalako Lamlungu, kuti adzapemphereredwe, ndipo ine ndinaganiza kuti izo zikhoza kupweteka ina ya mipingo inayo, kotero ine ndinangozisiya izo zokha.

16 Tsopano, usiku wathawu ine ndinalengeza kuti usikuuno ife tipempherera odwala pano. Ndipo ngati Mulungu alola, ife mwinamwake mawa usiku kapena usiku wotsatira, umodzi, tidzapempherera odwala kenanso. Kotero ine ndikudalira kuti izo zikhala zabwino, kuti Ambuye achiritsa aliyense amene akudwala pano usikuuno.

17 Ndipo ine ndikukuuzani inu, mzanga wofunikira, pamwamba pa zinthu zonse ine ndikudalira kuti odwala tchimo achiritsidwa usikuuno. Mukuona? Ngati Ambuye

angakuchiritseni inu ku matenda anu, inu mwinamwake, ngati inu muti mudzakhale moyo nthawi iliyonse, inu mudzadwala kenanso. Mukuona? Koma Moyo Wamuyaya ndi umene ife tikuwufunafuna, uko nkulondola, pakuti ndiwo—ndiwo machiritso enieni. Ndipo ine ndikudalira kuti ngati pali winawake pano amene siwokhulupirira mwa Khristu, akhala wokhulupirira usikuuno.

18 Ndipo ngati inu muli pano ndipo simunabadwe mwatsopano, kapena simunalandire Mzimu Woyera, kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, ine ndikudalira kuti uno ukhala usiku umene izo ziti zichitike.

19 Ngati inu muli wobwerera mmbuyo, ine ndikuyembekeza kuti Ambuye Yesu achita chinachake chenicheni kwambiri usikuuno, kwa inu pano, ndi kutenthetsa—kutenthetsa mtima wanu mwanjira yotero, mpaka inu mungobwerera ku chiyanjano Chake kenanso, chifukwa Iye akuyembekezera, ndi mikono yotambasulidwa, akudikirira.

20 Ine ndinalalikira zaka zina zapitazo pa ulaliki wawung'ono nthawi ina, uko ku Angelus Temple, pamene iwo anali ndi chisangalalo cha chipentekoste, zaka fifite za chisangalalo. Ine ndikukumbukira usiku woyamba, umene ine ndinalalikira pa chiyero, chimene ine ndimakhulupiriramo. Ndipo ine ndinakhala ngati sindinalinge kutero, koma, inu mukudziwa, kumangowadula anthuwo, ndi momwe anthu anali atachoka pa pentekoste yapachiyambi. Monga pamene, chiyambi choyamba, pamene Mzimu Woyera unagwa, momwe anthu amenewo ankakhalira moyo, zomwe iwo anachita, zaka fifite zapitazo!

21 Ine ndinati, "Oh, ife tachokera kutali. Ife tiri ndi mabungwe akuluakulu kuyambira pamenepo, nyumba zazikulu zabwino, ndi alaliki opukutidwa-mwapamwamba." Ine ndinati, "Ndikudabwa ngati ife tikadali ndi mdalitso wa chipentekoste umene ife tinali nawo nthawi imeneyo?" Mukuona? Mukuona? Ine ndinati, "Zinkakhala kuti, athu—alongo athu ankabwera ku tchalitchi, izo zinali zamanyazi kuti mmodzi wa iwo azikhala ndi tsitsi lalifupi, ali ndi zodzipakapaka, kapena chinachake chonga izo. Koma, izo, iwo akhala ngati alekerera zigwiriro penapake."

22 Ndipo kotero panali mzanga, amene, iye ndi m'bale wa chipentekoste nayenso, ndipo ambiri a inu mukhoza kumudziwa iye. Dzina lake ndi William Booth-Clibborn. Chabwino, ambiri a inu mukumudziwa iye.

23 Ndipo M'bale Booth ndi mzanga wapamtima, kokha kuti ife sitimagwirizana pa ziphunzitso, chifukwa iye ndi wotero—woganiza za Chikalvini mpaka iye amaganiza mondipyola ine. Kotero ine ndikhoza kungoganiza Chikalvini bola ngati icho chikukhala mu Baibulo. Mukuona? Ndiyeno pamene icho

chichoka mmenemo, icho chimadutsa kuganiza kwanga; ine sindimathanso kuganiza.

24 Chotero ine ndinamuwona iye pa nsanja. Kotero pamene ife tinachoka pa nsanja, iye anakomana nane kunja uko, ndipo iye anandiyang'ana ine. Iye anati, "Tsk, tsk, tsk, tsk, tsk. Manyazi pa inu. Uthenga wa chilamulo woterowo. Inu mumadziwa bwinoko kuposa zimenezo." Iye anangonding'amba ine, inu mukudziwa.

25 Ndipo tsiku lotsatira ine ndinalalikira pa *Mwanawankhosa Ndi Nkhunda*. Ndipo chotero Ambuye anadalitsa kwenikweni uthenga wawung'ono, wakale woswekawo. Ndipo pamene ine ndinatuluka, iye anali akupukuta maso ake, inu mukudziwa. Iye anati, "Izo zinali zabwino, koma zophweka kwambiri." Zophweka kwambiri! Ine ndinati . . . "Izo zinali zabwino," anati, "koma zophweka kwambiri." Iye anali chotero . . . Iye akhoza kulalikira mu zinenero seveni, inu mukudziwa, kotero kuyankhula kwanga kwakung'ono kwaku Kentucky kunali kophweka kwambiri kwa iye kumene makhalidwe anga abwino kwambiri sakanamukhudza iye, paliponse, inu mwaona.

26 Kotero umo ndi pafupifupi momwe ine ndikuyenera kuyankhulira: mophweka. Ine ndimakhulupirira kuti Uthenga ndi wophweka. Baibulo linati, "Ndi wophweka kwambiri kuti chitsiru chisamalakwitse." Mukuona? Kotero basi—basi zonse zimene inu mukuyenera kuchita ndi kukumbukira ABC. Inu mukudziwa chimene izo zimayimirira? Nthawizonse Muzimukhulupirira Khristu. Ndizo zonse zimene inu mukuyenera kuchita. Izo zikukhazikitsa icho. ABC, ndipo ndinu wophunzira kwathunthu, monga momwe ine ndikudziwira.

27 Kotero, tsopano, pali anthu amene ayima, ndipo ine ndikuyamikira zimenezo. Ndipo tsopano ine sindinabwere konse ku—kudzalalikira. Ine ndipempherera odwala. Koma, kuti ndipeze maziko pang'ono, ndiyankhule pa Malemba.

28 Ine ndikuganiza ndinakhala ngati ndinalalikira nkumalizitsa zonse, mmawa wina, kwa M'bale Fuller. Ine ndinatchula Life Tabernacle, kapena chinachake. [M'bale akuti, "Faith Tabernacle."—Mkonzi]. Faith Tabernacle, ine ndikuganiza ine ndinawagwira iwo usiku wina. Ine ndisanafike ku tchalitchi, m'busayo kapena winawake anali atanditumizira ine mawu, anati, "Kuti, anthu awa amakonda kupita kukagona usiku." Kotero ine sindimalalikira kawirikawiri mopitirira maora sikisi kapena eyiti, kotero ine sindimafika mopitirira pamenepo. Kotero, uko kwa M'bale Outlaw, usiku wina, ine ndinaganiza kuti iye anali woti watsala pang'ono kuti andichotsepo ine pa guwa. Kotero ine kulibwino ndizitenge izo mophweka usikuuno, kutali komwe kuno, ndipo ena a inu mukuchokera kutali kwambiri.

29 Tsopano, nkwabwino kukhala kuno. Ndipo tisanawayandikire Mawu tsopano, tiyeni tiyankhule kwa

Mlembi.

30 Winawake anati, osati kale kwambiri, ine ndinali ku Fort Wayne Gospel Tabernacle, B. E. Rediger. Iye anali munthu wamkulu wa Mulungu, amene anafa zaka zapitazo, amene Ambuye anamudalitsa kwenikweni m'bale ameneyo. Iye anali munthu wamphamvu wa chikhulupiriro. Ine ndinali mnyamata wamng'ono, ine ndinkakonda kukhala ndi Paul Rader uko, ndipo mtumiki wamng'ono chabe.

31 Ndiyeno mwana wamkazi wa M'bale Rediger anasokonezeka mmalingaliro, anapenga. Tsiku lina iye anali kumbuyo mu chotchinga changa cha malasha kumusi uko, mmawa wina wa Isitara. Ndipo iwo anandiwuza ine, "Mtsikana wina wamisala, kumbuyo uko mu tchalitchi." Ndipo ine ndinali nditangobwera kumene kuchokera ku msonkhano. Ine ndinabwerera kumeneko, ndipo ndinakapeza kuti anali mwana wamkazi wa B. E. Rediger, ndi Mlongo Rediger, atakhala pamenepo. Mtima wanga unakhala ngati wandilephera ine.

32 Ndipo iye anali atayima pamenepo, akupesa tsitsi lake lokongola ndi zala zake zazitali, akufuula, "Tambala tambala. Kobidi kobidi." Mkazi wamng'ono wokongola. Pamene . . .

33 Ndinagwada pansi pamenepo, ndipo ndinati, "Ambuye Yesu, muchitireni chifundo iye." Zinali zimenezo basi. Iye anakwatiwa ndipo ali ndi ana awiri kapena atatu tsopano, ali bwino basi. Mukuona? Ndipo chisomo choterocho, ndipo zophweka.

34 Ife—ife timangoyang'ana panja ndi kufikira pamwamba pa Iye, moona mtima, kumayesetsa kuti tipeze chimene chiri pafupi kwambiri ndi ife monga choncho. Ife, mophweka basi; kukhulupirira; kukhala ndi chikhulupiriro; osakayikira ayi.

35 Ine ndinali ndi msonkhano kumeneko. Ine ndamuiwala m'bale wa Chipentekoste amene ali ndi ulamuliro wa kachisiyo tsopano. Ndipo ine ndinali ndi msonkhano kumeneko. Ndipo kunali nyimbo iyi, *Kungo Khulupirira,* inalembedwa ndi Paul Rader. Ndipo iye anali Mkhristu wodabwitsa chotero ndi mtumiki wopambana wa tsiku lake. Ine ndinali nditakhala mu chipinda chaching'ono chowerengera. Ndipo iwo anali akuyimba, kuti ine ndibwere pa nsanja, ndi iyo; imene iwo ali nayo, kuzungulira dziko. Ndipo ine—ine ndinali nditakhala mmenemo, ndipo nkumadziwa kuti mowerengera momwemo ndi mmene Paulo anapeza kudzoza kuti alembe nyimboyo. Ndipo apa iyo inabwera, *Kungo Khulupirira*. Oh, izo zinangowotcha mtima wanga!

36 Utatha msonkhanowo, panali zinthu zazikulu zingapo zimene Ambuye Yesu wathu anali atachita mu msonkhanomo. Ine ndinabwerera kumeneko, cha ku mbali ya malowo, ndipo ndinkadikirira.

Ndipo apo panali mwamuna amene analowa mkati. Iye anati, "Bambo Branham?"

Ndipo ine ndinati, “Inde, bwana.”

37 Iye anati, “Ine ndimakonda kukumvani inu mukuyankhula, koma,” anati, “galamala yanu ndi yoyipa kwambiri.”

Ine ndinati, “Inde, bwana. Ine ndikudziwa zimenezo.”

Iye anati, “Inu mumanena zina za zinthu zoyipa kwambiri.”

38 Ine ndinati, “Inde, bwana. Uko nkulondola.” Ine ndinati, “Ine sindinapeze mwayi woti ndipeze maphunziro.” Ine ndinati, “Ndinaleredwa m’banja la ana teni. Makolo osawuka, ndipo ine ndinkayenera kuyamba ntchito molawirira, kuti ndizithandizira kusamalira banja ili. Ine sindinapeze ngakhale maphunziro a sukulu ya galamala.”

Iye anati, “Icho si chowiringula tsopano. Inu ndi mwamuna.”

39 Ine ndinati, “Chabwino, ine ndi wotanganidwa kwambiri ndi ntchito ya Ambuye tsopano, ine ndiribe mpata.”

40 Anati, “Komabe, inu mukhoza kutenga maphunziro omangowerenga.” Anati, “Tsopano, mwachitsanzo, usikuuno, kunja uko, inu munati, ‘Anthu nonse inu mukudutsa pa guwa ili.’”

41 Ine ndinati, “Chabwino?” Ine sindinadziwe kusiyanitsa kulikonse. Ine ndinati, “Kodi icho si chimene iye ali?”

42 “Ndithudi ayi.” Anati, “Inu mumayenera kunena kuti ‘guwa.’” Ine ndinati . . . Iye anati, “Inu . . . ”

43 Ine ndinati, “Chabwino, chabwino.” Ndi chinachake chimene ine ndinachitchula molakwika, kapena chinachake.

Iye anati, “Chabwino, inu simumalidziwa basi Baibulo lanu.”

44 Ine ndinati, “Chabwino, izo—izo zikhoza kukhala chomwecho, koma ine ndimamudziwa Mlembiyo mwabwino kwenikweni.” Ine ndinati, “Ndi zimenezotu.”

45 Inu mukudziwa, Ilo silimanena kuti, “Kulidziwa Bukhu Lake.” Koma, “Kumudziwa Iye ndi Moyo.” Mukuona? Satana amawadziwa Mawu Ake. Koma, “Kumudziwa Iye, Mlembi wa Mawu,” mwaona.

46 Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano pamene ife tikuyankhula kwa Iye mwanjira yathu yodzichepetsa. Tsopano, ndi mitu yathu yoweramitsidwa, mitima yathu, ndi iyo, kodi chiripo chopempha chapadera chimene inu mukufuna kuti ife tikukumbukireni? Kwezerani mmwamba dzanja lanu kwa Mulungu. Basi mu mtima mwanu mugwire chopempha chanucho, munene, “Ambuye, ine ndikusowa chipulumutso. Ine ndikusowa machiritso. Ine—ine ndikusowa chinachake.” Mulungu amvetsetsa.

47 Atate athu Akumwamba, pamene ife tikuyandikira Kukhalapo Kwanu koyera usikuuno, mu Dzina la Ambuye Yesu, ife tikubwera mu Dzina Lake chifukwa Iye ananena,

kuti, “Ngati inu muwapempha Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho.” Tsopano, ife tikudziwa kuti sitingakhoze kubwera mu dzina lathu lomwe. Ife sitingathe kubwera mu dzina la mpingo wathu, mu dzina la abusa athu, kapena mu dzina la bungwe lathu, ndipo nkuyembekeza kuti timvedwa. Koma ife tiri ndi chitsimikizo kuti ngati ife tibwera mu Dzina la Ambuye Yesu, kuti Iye anatilonjeza ife kuti ife tidzamvedwa.

48 Ndipo ine ndikupemphera, usikuuno, Atate Akumwamba, kuti pamene ife tasonkhana pano mu kachisi wamng’ono uyu amene waperekedwa ku utumiki Wanu, amene wantchito Wanu, M’bale wathu O’Donnell, akutumikira pa nthawi ino, kuweta nkhosa zimene zikuyendera ku mbali ino ya dziko, ine ndikupempha madalitso Anu pa m’busa uyu ndi pa banja lake, pa mpingo ndi nkhosa zonse zimene zimadya pa msipu uwu.

49 Ine ndikupempherera mpingo uliwonse umene wayimiridwa pano, kwa anthu onse. Ndipo kwa iwo amene si Akhristu ine ndikupemphera kuti usikuuno iwo akhale Akhristu. Ine ndikuwapempherera amuna amalonda amene ali pano, M’bale Rose, M’bale Williams, ndi ena ambiri, chifukwa cha msonkhano waukulu umene ukubwera kumeneko. Kuti, kukondoweza kwakung’ono uku kwa masiku ochepa awa ku Phoenix, ndi Tempe, ndi Sunnyslopes, ndi kudutsa mdziko kuno, kupangitse Akhristu ambiri kugwira mwatsopano, obwerera mmbuyo ambiri abwerere kwa Mulungu, ochimwa ambiri kubwera kwa Khristu, odwala ambiri kuchiritsidwa. Perekani izi, Atate.

50 Yankhulani kupyolera mwa ife, kupyolera mu Mawu usikuuno, Choonadi. “Mawu Anu ndi Choonadi.” Chiritsani odwala onse ndi osautsika, kwa zonse zathupi ndi zauzimu. Manja awa amene anakwera mmwamba ali ndi chosowa, Ambuye, ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mupereke zonsezo usikuuno, kudzera mwa Yesu Khristu, Ambuye wathu. Ameni.

51 Tsopano, ambiri a inu mumakonda kuwerenga Malemba ndi iwo amene akuwerenga. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge malo awiri usikuuno. Amodzi a iwo akupezeka mu Marko, mutu wa 16, ndipo ife tiyambira pa ndime ya 14. Ndipo ena akupezeka mu Yohane Woyera. Kapena, ine ndikuganiza ndi pamene ine ndinalemba. Ndiroleni ine ndiwone, poyamba. Inde. Yohane Woyera 14:12 ndi pamene Lemba lachiwiri. Ndipo tsopano mu Marko Woyera, mutu wa 11 ndipo kuyambira ndi ndime ya 14. Ndi Yohane Woyera 14:12. Tsopano ife tikufuna kuti timvetsere mwatcheru ku kuwerengako, chifukwa Mawu a Mulungu ndi amene ife tikufuna kuti tiwamve. Poyamba, Marko 16.

> Ndipo atatha *kuwonekera kwa leveniwo pamene iwo anakhala kuti adye, ndipo anawadzudzula iwo chifukwa cha kusakhulupirira ndi kuuma kwa*

*mtima, chifukwa iwo sanawakhulupirire iwo amene anamuwona iye iye atatha kuwuka.*

*Ndipo iye anati kwa iwo, Pitani inu ku dziko lonse, ndipo mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse.*

*Iye amene adzakhulupirira nabatizidwa adzapulumutsidwa; koma iye amene sadzakhulupirira adzalangidwa.*

*Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira; Mu dzina langa* iwo adza*tulutsa ziwanda; iwo adzayankhula ndi malirime atsopano;*

*Iwo adzatola njoka; ndipo ngati iwo adzamwa chinthu chakupha chirichonse, icho sichidzawapweteka iwo; iwo adzayika manja pa odwala, . . . iwo adzachira.*

*Kotero . . . Ambuye atatha kuyankhula ndi iwo, iye analandiridwa kumwamba, ndipo anakakhala pa dzanja lamanja la Mulungu.*

*Ndipo iwo anapita, ndipo anakalalikira konsekonse, Ambuye akugwira nawo ntchito, akutsimikizira mawu ndi zizindikiro zikuwatsatira. Ameni.*

52 Yohane 14:12, Yesu akuyankhula.

*Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Iye amene akhulupirira pa ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita; ndipo ntchito zazikulu zoposa izi iye adzazichita; chifukwa Ine ndikupita kwa Atate anga.*

53 Ine—ine ndikufuna kuti nditenge ngati phunziro, ngati Ambuye alola, pa *Kutsimikizira Kwa Kutumidwa*, ngati mutu, ndipo kuti ndingoyankhula. Ine ndiri ndi Malemba pang'ono ndi zolemba zomwe ndalemba, zimene zikhoza kutithandiza ife mopitirira. Tsopano: *Kutsimikizira Kwa Kutumidwa*.

54 Tsopano, ine ndikuganiza kuti chirichonse chimayenera kutsimikiziridwa. Ngati mungati mumange nyumba, iyo ikanayenera kumangidwa molingana ndi ndondomeko, kapena iwo sakanatsimikizira kuti nyumbayo imangidwe; ndipo inu mukanayenera kuti muigwetsenso iyo, nkuyimanganso iyo.

55 Ndipo ine ndikuganiza, nanenso, kuti ngati inu mukanamayenda mu msewu, ndipo, kapena kunja pa ntchito yanu, ndipo winawake nkubwera kwa inu nkudzati, "Ndine wapolisi waku United States. Tsopano ndikukumanga iwe, mu dzina la ofesi yanga." Tsopano, inu muli ndi ufulu wonena kwa munthu ameneyo . . .

56 Ngati iwe utamuyang'ana iye, nkupeza kuti wavala yunifolomu, ndi baji itayikidwa pa iye. Izo komabe sizingamupange iye kukhala wapolisi wa United States. Wachinyengo aliyense akhoza kuvala zimenezo. Inu mukhoza

kugula baji chakuno apa, pafupifupi, mu sitolo ya teni senti. Kupita ku zogulitsa zosiyanasiyana ndi kukapeza yunifolomu, kapena chirichonse. Izo sizimamupanga iye kukhala wapolisi wa United States.

57 Kuti adzizindikiritse yekha, iye akuyenera kukhala ndi mapepala ake ndi chisindikizo pa izo, kuti atsimikizire neno lake lakuti iye ndi wapolisi wa United States. Kapena, iye si kanthu mpaka iye atatsimikiziridwa kuti ali chimenecho. Iye watsimikizira utumiki wake, ndipo iye amachita izo mwa chikalata chosindikizidwa, cholengeza, kuwonetsera kuti munthu uyu analumbirira. Ndipo iye wakhala... Kutumidwa kwake kunasindikizidwa ndi chisindikizo cha United States, ndipo kenako pamwamba pa dzina lake. Ndipo izo zimamupanga iye pamenepo, kaya iye wavala baji, kapena iye wavala yunifolomu, bola ngati iye wanyamula pepala ili, iye ndi wapolisi, ndipo umenewo ndi utumiki wake. Baji yokha ndi yunifolomu sizingagwire ntchito.

58 Ife timapeza, nthawi zochuluka kwambiri, mwa asilikali. Ine ndawamvapo abale anga ndi ambiri a iwo amene anali kutsidya kwa nyanja. Kuti, nthawi zambiri, achi Japan ndi achi German, ndi mayiko ena achilendo amene ankalimbana nafe mu nkhondo, ngati akanatha kumunyamula msilikali wakufa, kenako nkutenga mmodzi wa asilikali awo amene yunifolomuyo ikanamukwana, bwanji, iye amakhoza kutsanzira msilikali wa Amerika. Ndipo iye ankayenera kuti azindikiritsidwe bwinobwino, kapena iwo sakanakhulupirira konse yunifolomu yake kapena mwinamwake chizindikiritso chake chimene iye anali nacho pakhosi pake. Iye ankayenera kuti adziwike kuti iye anali msilikali wa ku America, chifukwa iye akanakhoza kukhala kazitape mosavutikira. Kazitape wotchipa aliyense akhoza kuvala yunifolomu ya United States.

59 Ndipo ife tikupeza kuti mmayendedwe onse a moyo. Ife tikupeza kuti, lero, mwinamwake pa msewu. Ife timamva anthu ambiri akunena kuti iwo ndi Achimerika.

60 Ndipo kuno nthawi yina kale, ndikutuluka kuchokera ku ofesi ya Woyang'anira kokhala asilikali imene inali kumeneko ku Jeffersonville, Ine ndinkayenda mmawa wina, ndikupita kolondera. Ndipo apo panali—munthu wovala bwino akuyenda mu msewu, ndudu yayikulu mkamwa mwake, wogwira ntchito m'boma. Ndipo iye anayang'ana pa ine, molawirira mmawa, atavala magalasi a dzuwa. Ine ndinati, "Mmawa wabwino, bwana."

Iye anayang'ana pa ine, ndipo anati, "Huh!" Anayamba kumayenda.

61 Tsopano, ine ndinaganiza kwa inemwini, ine sindiri... ndisanene kanthu, koma mu mtima mwanga, iye sanali kwenikweni wa Chimerika, chifukwa mfundo za Amerika siziri

zokhazikitsidwa pa zinthu zotero monga zimenezo. Kulondola. Chiyanjano, ndi kulolerana, kufunirana zabwino.

62 Ndipo tsopano, inu mwaona, onse amene amakhala mu Amerika si Achimerika. Muli azondi, achikominisi, ndi china chirichonse. Ndipo njira yokhayo imene iwo angakhoze kudziwika kwenikweni, kaya iwo akulondola kapena ayi, ndi mwa chawo kwenikweni, chimene chiri mkati mwa iwo, kaya mtima wawo uli mu Amerika kapena bukhu lawo la mthumba chabe. Mukuona?

63 Izo zimatengera chimene icho chiri. Wachinyengo aliyense akhoza—akhoza kukhala ndi izi zomwe zimatchedwa kuti zoyenereza, ndipo komabe osakhala munthu weniweniyo.

64 Ndi chifukwa chake ine ndimakhulupirira kuti onse amene amabwera mnjira yathu, akudzitcha okha Akhristu, akazembe otumizidwa kuchokera Kumwamba, iwo akuyenera kumakhala ndi kutsimikizira kwa utumiki wawo. Ine ndikukhulupirira kuti pakuyenera kukhala kutsimikizira kwa utumiki wawo.

65 Tsopano, ife tikuzindikira kuti Yesu ananena apa, mu Marko mutu wa 16, kuti onse amene Iye anawatumiza ku utumiki adzakhala ndi chitsimikiziro. "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira."

66 Tsopano, Iye sananene kuti, "Iwo, mwinamwake zidzawatsatira, kapena izo zikhoza kudzawatsatira."

67 Iye anati, "Pitani inu ku dziko lonse." Tsopano, winawake amafuna kuti awudulire utumiki umenewo, ku zaka thuu sauzande zapitazo. Koma Iye anati, "Dziko lonse, kwa cholengedwa chirichonse. Zizindikiro izi zidzatsatira mu dziko lonse, ndi kwa cholengedwa chirichonse." Mukuona? Ndipo zimenezo zinali zizindikiro zimene zinali zoti zitsatire, kuti zitsimikizire kuzindikiritsidwako.

68 Baibulo linati, "Uthenga sunadze kwa ife mu mawu okha, koma kupyolera mu mphamvu, mawonetseredwe a Mzimu Woyera." Mwa kuyankhula kwina, "Ndi Mzimu Woyera ukutenga Mawu a Mulungu ndi kuwapanga Iwo kuwonetseredwa." Mukuona? Ndipo, mwanjira ina, njira yokhayo imene zizindikiro za Marko 16 zingakhoze kumutsatira wokhulupirira ndi yakuti Mzimu Woyera Mwiniwake umawatenga Mawu a Mulungu ndi kuwawonetsera iwo kwa anthu. Ndi zimenezotu. Tsopano, chikhulupiriro chimawapangitsa Mawu amenewo kukhala amoyo. Mukuona?

69 Mawu ndi Mulungu. "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu." Ndipo kenako Yesu anati, "Ngati inu mukhala mwa Ine, ndi Mawu Anga mwa inu, pemphani chimene inu mukufuna, icho chidzachitidwa kwa inu." Mukuona? Kumeneko ndi kukhala ndi Khristu mu Mawu. Musamapite kumanja kapena kumanzere, muzikhala ndi Iwo. Mukuona? Ndiyeno Iwo sali kwenikweni

mawu anu ndiye, Iwo ndi Mawu Ake, ndipo Mawu Ake amakhala ndi mphamvu ndi ulamuliro kuseri kwa Iwo. Tsopano, ndipo ngati Mzimu Woyera, umene uli Mawu a Mulungu, kapena mphamvu ya Mawu a Mulungu, ubwera mkati ndi Mawu a Mulungu, Iwo udzapangitsa Mawu a Mulungu kudziwonetsera Okha.

> . . .*Pitani inu ku dziko lonse, ndipo* mukawonetsere *Uthenga kwa cholengedwa chirichonse.*
>
> *Ndipo iye amene adzakhulupirira nabatizidwa adzapulumutsidwa;. . .iye amene sadzakhulupirira adzalangidwa.*
>
> *Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira;. . .*

70 Ndi malo okongola chotani amene iwo ali! Ngati ife titangopita mwakuya tsopano ndi kumvetsera: izo zinali zoyenereza zimene zinali zoti zizipachikika pa munthu aliyense amene anapita kumakalalikira Uthenga. Ndipo palibe munthu amene ali ndi ufulu woti azilalikira Uthenga wopanda ubatizo wa Mzimu Woyera. Yesu sanamulole Petro, Yakobo, Yohane, aliyense wa iwo onse, kukalalikira Uthenga mpaka iwo atadikirira mu mzinda wa Yerusalemu kufikira Mzimu Woyera utawadzaza iwo, chifukwa ndi Mzimu Woyera umene umawapangitsa Mawu a Mulungu kuti achite ntchityoo. Mukuona?

71 Tsopano, Mawu omwewo ali amoyo basi usikuuno monga Iwo ankakhalira mu ora limene Iwo anayankhulidwa. Mukuona? A. . .Zonse zimene ife tikusowa ndi Mzimu Woyera kuseri kwa Mawu, kuwapangitsa Iwo kuti achite ntchitoyo ndi kuwonetsera mphamvu imene Iwo analonjeza. Mdalitso uliwonse umene Mulungu analonjeza, chirichonse chimene Iye ananena, chikhoza kubweretsedwa ku moyo ngati Mzimu Woyera uli kuseri kwa Mawu, chifukwa icho ndi chinthu chimene chimafulumizitsa Mawu ndi kuwapatsa Iwo moyo. Mukuona? Ndipo tsopano ife tikudziwa kuti uko nkulondola.

72 Yesu anati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira onse amene Ine ndidzawatuma." Ena, amakana. Ndizo zonse. Ndithudi.

73 Wosakhulupirira aliyense, wotsutsa Mawu aliyense, akhoza kubwera motsatira ndi chizindikiritso cha chipembedzo chinachake, bungwe lina lopangidwa ndi munthu kapena chinachake, nkumati, "Ndine wa Presbateria, Chilutera, Baptisti," chirichonse chimene chingakhale. Iye akhoza kudzizindikiritsa yekha mophweka mu chiyanjano cha mpingo wa chipembedzo womwewo, chifukwa cha ziyenerezo zake. Koma ziyenerezo zake zimangobwera kokha kuchokera ku bungwe limene linapangidwa ndi lingaliro ndipo osati Mawu a Mulungu.

74 Koma Mulungu, ngati iye watumidwa kuchokera kwa Mulungu, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Mukuona? Yesu ananena chomwecho. Mukuona? Mukuona?

75 Izo ndi, mwina, inu mutenga zimene bungwe linalake linanena, zimene lingaliro linalake lopangidwa ndi anthu linanena. Iwo adzalalikira chiphunzitso cha lingaliro limenelo, ndipo kenako zimenezo ndi zoyenereza zawo ku gulu la madikoni, kapena chirichonse chimene icho chiri, kuti iwo amayima mu chiyanjano chabwino ndi bungwe limenelo. Ine ndiribe kanthu kotsutsa izo, mumvetsetse.

76 Koma ine ndikungotetezera zimene Yesu ananena. Mukuona? Iye anati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Ndipo Yesu anati, mu Yohane Woyera 14:12, "Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu." Ndizo, "Mwamtheradi, mwamtheradi, Ine ndinena ndi inu, iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita."

77 Ndipo munthu angakhulupirire bwanji kuti iye watumidwa kuchokera kwa Mulungu, ndipo kenako nkutembenuka ndi kukana utumiki womwewo umene Mulungu anati ukanadzatero, kuti ukanadzakhala chizindikiritso cha munthu aliyense amene Iye anamutumiza? Munthu anganene bwanji kuti, "Kulibe chinthu choterocho monga ubatizo wa Mzimu Woyera"? Munthu anganene bwanji kuti, "Kulibe chinthu choterocho monga machiritso a odwala"? Munthu anganene bwanji kuti, "Kulibe chinthu choterocho monga kuyankhula mmalirime, kutulutsa ziwanda"? Pamene, izo zinali zoyenereza zomwezo zimene Yesu anazimata pa wokhulupirira aliyense amene akanati, Iye anamutumiza. Umenewo ndi ulamuliro.

78 Tsopano, inu mukhoza kupita ku sukulu ndi kukatenga Ph.D., ndi LL.D., ndi china chirichonse chimene inu mukufuna kuti muchite, ndipo izo zonse nzabwino. Izo ndi zizindikiritso zanu ku bungwe limenelo. Ndipo izo nzabwino. Ine ndiribe kanthu kotsutsa izo; ndikanakonda ine ndikanakhala nazo.

79 Koma chizindikiritso chimene Yesu, pamene Iye atumiza munthu, ndi, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Mukuona? Zimenezo ndi zizindikiritso zosonyeza kuti iye watumidwa ndi Mulungu. "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira."

80 Tsopano, monga ndinanenera, mwamuna aliyense wachinyengo akhoza kutenga yunifolomu kapena baji, koma chimenecho si chomuyenereza kwenikweni. Ndi zoyenereza zimene zimawerengeredwa, osati yunifolomu kapena baji. Ndipo pali anthu ambiri. . .Ndipo izo ndi zoipa kwambiri kuti ine ndikuyenera kunena ichi, koma icho ndi choonadi. Ife tikuyenera kukhala owona mtima. Pali ambiri a. . . anthu athu Achipentekoste, amene akungovala baji ndi

yunifolomu, mwaona, chifukwa chakuti iwo amakhala mosiyana kwambiri ndi chimene kwenikweni wachipentekoste amayenera kumakhalira, mpaka pali—palibe kanthu kwa izo. Ndizo zonse. Ndipo izo zimangobweretsa chitonzo pa Cholingacho. Uko nkulondola. Izo zimawapangitsa anthu kukayikira.

81 Koma Yesu anapereka kutsimikizira, kuti izo zikanadzakhala zabwino, chifukwa, "Zizindikiro izi zikanawatsatira okhulupirira." Icho ndi chinthu chimodzi. Mzimu Woyera unayang'ana pansi kudutsa mu mtsinje wa nthawi ndipo unawona kuti anthu akanadzapotoza Mawu Ake ndi kuyambitsa *ichi, icho*, ndi *chinacho,* kotero Iye anazipanga izo momveka bwino kwambiri ndi motsimikiza kwambiri kotero kuti palibe njira yopitira mozungulira izo. Iye anati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Tsopano, ife tikudziwa izo kuti ndi zoona.

82 Wosakhulupirira akhoza kutenga zoyenereza zachipembedzo izi, koma izo si zimene zimamupanga iye kukhala munthu wotumidwa kuchokera kwa Mulungu. Iwo amayenda kuzungulira kuno ndi mitundu yonse ya mabuku mu nkhwapa mwawo, kuzungulira dzikoli, ndipo *ichi,* Yehova ndi *ichi*, ndi *chakuti-ndi-chakuti*, ndi zonse *izi*, *chinacho,* koma izo sizimapanga izo kukhala chomwecho. Ayi, bwana.

83 Yesu anati, "Inu muwayese iwo ndi Mawu." Uko nkulondola. Mawu, "Zizindikiro izi zidzawatsatira."

"Kodi inu mumakhulupirira mu mphamvu ya Mulungu?"

84 "Oh, wathu—mpingo wathu umaphunzitsa zimenezo. . . " "Mpingo wathu," izo ziribe kanthu kochita ndi Iwo.

85 Ndi chimene Mawu a Mulungu amanena. Mukuona? Eya. "Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzapita." Mawu amoyo, oyankhulidwa ndi Mulungu wamoyo, akuyenera kukhala mwa munthu wamoyo. Ndipo zingatheke bwanji kuti mwamuna kapena mkazi, amene amadzinenera kuti ali ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, akane chimene Mulungu ananena mu Mawu Ake? Chifukwa, ndi Mzimu Woyera womwewo umene unalemba Mawu, ndi Mzimu Woyera womwewo umene ukuyankhula kupyolera mwa munthuyo. Uko nkulondola. Izo zikuyenera kukhala chomwecho. Iye sangathe, iye sangathe kuchita izo. Inde, bwana.

86 Tsopano, koma, kuti, munthu akhoza kubwera ndi kudzati, "Ine ndiri ndi khadi la chiyanjano. Ine ndi wa mpingo *uwu* kapena mpingo *uwo*." Izo sizimapangabe izo kukhala zolondola. Iye akhoza kukhala ndi Ph.D., LL.D., ndi china chirichonse kuchokera ku sukulu ina yaikulu. Izo nzabwino. Palibe chotsutsa izo. Izo zikhoza kukhala zabwinobe. Ine ndiribe kanthu kotsutsa izo. Koma ngati Mulungu anamutuma iye. . . Ndipo ngati iye akana kutuma uku *Apa* . . . Ngati iye ali ndi *izo* kuwonjezera *Ichi,*

zopambana. Koma ngati iye ali ndi *icho* popanda *Ichi*, ndiye icho si chabwino. Mukuona? Uko nkulondola.

87 Nzabwino ngati munthu avala yunifolomu ndi baji nkukhala ndi zomuyenereza. Chabwino. Koma iye akhoza kuvala yunifolomu ndi baji popanda zomuyenereza. Uko nkulondola. Kotero icho ndi chitsimikiziro cha utumiki, icho chikuyenera kuyima. Icho chikuyenera kuchita, mosakayikira.

88 Wosakhulupirira uyu amene angadutsepo ndi kunena kuti, "Chabwino, ine sindimakhulupirira kuti pali chinthu choterocho chonga ubatizo wa Mzimu Woyera. Masukulu athu aphunzitsa kuti—kuti masiku amenewo anapita. Ife sitikusowa kuti tizikhala ndi zimenezo panonso." Ndipo alipo ochuluka kwambiri a iwo amene amakhulupirira zimenezo. Alipo ochuluka kwambiri a iwo amene amakhulupirira zimenezo moonamtima, amuna abwino, ndi chifukwa chakuti iwo amamvetsera ku sukulu mmalo mwa Mawu a Mulungu. Uko nkulondola ndendende.

89 Kuno nthawiyina kale, pa malo enaake, panali a—a—mkazi. Iye anali ndi mwana wamwamuna. Ndipo iye anali, anali ndi kuyitana kwa Mulungu mmoyo wake; iye ankawoneka kuti anali nako. Ndipo mayi wokalamba wosawukayo ankafuna kuti amutumize iye ku sukulu, kuti akachite zonse zimene iye akanatha zoti zimumangirize iye. Chimene, icho ndi chinthu chabwino kuchichita. Koma iye anamutumiza iye ku sukulu yolakwika. Iye anamutumiza iye ku malo kumene iwo anayamba kuphunzitsa mosiyana ndi Mawu a Mulungu, ndipo iye anapitirira. Iye ankachapa, kuti amutumize iye ku sukulu, ndi zina zotero, ndipo nthawi yaitali inadutsa. Ndipo, potsiriza, iye sanabwere kunyumba kwa kanthawi.

90 Mayi wokalambayo anadwala. Iye anadwala kwenikweni, kwenikweni. Ndipo iye anafika poyipa kwambiri mpaka adokotala ananena kuti iye sakhala moyo, kuti iye ankayenera kuti afe. Kotero iye anapeza mmodzi wa oyandikana nawo kuti atumize telegramu kwa mwana wake wamwamunayo, kuti abwere kunyumba mwamsanga, chifukwa iwo anali akumuyembekezera iye kuti afe. Ndipo chotero woyandikana nayeyo anatumiza telegramuyo.

91 Ndipo—ndipo kotero mnyamatayo anakonzekera kuti azibwera. Ndipo patapita kanthawi, telegramu ina inabwera ndipo inati, "Usadandaule. Iwo ali bwino."

92 Kotero ndiye, miyezi ingapo itapita, mnyamatayo anabwera kunyumba kuti adzachezere amayi akewo. Ndipo—ndipo iye anati kwa iwo, akusangalala, ndipo—ndipo akuwauza iwo kuti iye anali ndi digrii yake ya Bachelor of Art, ndi zonse zomwe iye anali atachita, ndi momwe iye ankakhalira bwino ku sukulu. Ndipo iye anati, "Tiri pomwepo, amayi," anati, "Ine ndinayiwala kukufunsani inu." Anati, "Inu munanditumizira

ine telegramu, pafupifupi miyezi sikisi yapitayo, kuti ndibwere kunyumba." Anati, "Ine ndinali wokhumudwa kwambiri." Ndipo anati, "Ine ndinawopsyezedwa kwambiri ndi zimenezo." Ndipo anati, "Ine ndinakonzeka kuti ndizibwera. Ndipo kenako telegramu ina inabwera, kuti inu munali bwino. Inu munali mutachira. Ndipo ine ndinali wokondwa kwambiri ndi zimenezo. Amayi, ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu, kapena, amayi, ine ndikufuna kuti inu mundiwuze ine chimene chinachitika. Kodi adokotala anakupatsani mankhwala anji, nanga munali ndi dokotala wanji?" Anati, "Ine ndikufuna kuti ndipite ndi—ndi kukamuyamikira iye chifukwa cha ntchito yake yabwino."

93 Iwo anati, "Chabwino, mwana." Anati, "Dokotala Yesu anali Mmodziyo Amene anachita zimenezo."

Iye anati, "Amayi?"

94 Anati, "Dokotala Yesu." Iwo anati, "Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti*, msing'anga wanga, anabwera kuno, ndipo kutentha thupi kwanga kunali kutakwera kwambiri, ine ndinali nditasokonekera mmutu mwanga." Ndipo anati, "Iwo anati ine ndinafika poyipa kwambiri, kotero kuti ine ndinali woti ndifa." Ndipo iwo anati, "Iwe ukudziwa kumene kuli utumiki waung'ono uwo kuzungulira ngodyayo, kumusi uko pa kampita?"

"Inde."

95 Anati, "Anthu amenewo anali ndi msonkhano wa mapemphero kumusi uko usiku wina, ndipo iwo anati Mzimu Woyera unawauza iwo kuti abwere kuno ndi kudzandipempherera ine." Ndipo anati, "Sipanatenge nthawi iwo anadzandipempherera ine, malungo onse anathapo." Ndipo iwo anati, "Oh, mwananga!" Iwo anati, "Aleluya!" Iwo anati, "Ine ndachiritsidwa."

96 "Oh," iye anati, "amayi, amayi, kulimba mtimako! Bwanji, inu musamayanjane ndi anthu wonga amenewo." Iye anati, "Bwanji, inu simukuyenera kumawabweretsa anthu amenewo kuno."

Iwo anati, "Oh, bwanji, mwananga?" Anati, "Chabwino, ulemelero kwa Mulungu!"

97 Iye anati, "Amayi, musamanene zinthu zimenezo." Anati, "Bwanji, bwanji, inu mukundidzidzimutsa ine!" Mukuona? Anati, "Bwanji, inu simukuyenera kumanena zinthu zimenezo. Bwanji," anati, "anthu amenewo alibe maphunziro. Iwo samadziwa chirichonse cha Baibulo."

98 "Oh," iwo anati, "Ine ndikupempha kukhululuka kwako, mwana." Anati, "Iwo anabwera kumusi kuno komwe ndipo anandiwerengera kuchokera mu Baibulo, pamene ilo linati, 'Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati

iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.'" Anati, "Dikira. Ine ndawerengapo izo nthawi zambiri. Ine ndinalemba izo mu Baibulo langa. Ine ndipita ndikakuwonetse iwe."

"Oh, dikirani miniti yokha, amayi." Anati, "Ameneyo ndi Marko 16."

"Inde, ndi pamene izo ziri, wokondedwa," anati, "Marko 16."

99 Anati, "Oh, amayi," anati, "inu mwaona, anthu osauka amenewo, iwo samadziwa zabwino zirizonse." Anati, "Ife tinaphunzira ku sukulu kuti Marko 16, kuyambira mutu wa 9 mpakana, si wodzozedwa. Mukuona? Iwo si odzozedwa kwenikweni. Iwo anangowonjezeredwa."

100 Ndipo mayi wamng'onoyo anati, "Ulemelero kwa Mulungu! Aleluya!" Ndipo iye. . .

Mnyamatayo anati, "Amayi, inu mukutanthauza chiyani?"

Anati, "Ine ndimangoganiza."

Anati, "Mumaganiza chiyani, amayi?"

101 Iwo anati, "Ngati Mulungu angakhoze kuchita izo kwa ine ndi Mawu osadzozedwa, kodi Iye angachite chiyani ndi amene ali odzozedwa kwenikweni?" Kotero izo, uko nkulondola. Mukuona? Mukuona? Ndi zimenezotu. Oh, mai!

102 Vuto linali chiyani? Utumiki waung'ono uja kuzungulira pakona unali ndi choyenereza, mwinamwake osati Ph.D. kapena LL.D. Kapena. . .Koma iwo anali ndi zoyenereza za Mulungu, "Ndi zizindikiro izi zikuwatsatira iwo amene akhulupirira." Yesu anati ife tidzachita izo. Iwo—iwo anali ndi kutsimikizira kwa Mulungu. Iwo anali ndi utumiki Wake, kuti apite akayike manja pa odwala, ndipo iwo anachita zimenezo basi momwe Iye ananenera kuti azichitira, ndipo (iwo) Mulungu anawatsimikizira Mawu ndi zizindikiro zikutsatira. Chinali chitsimikiziro chakuti iwo atumidwa ndi Mulungu. Inde, bwana. Izo nzoona. Chabwino.

103 Tsopano, limenelo ndi phunziro labwino. Chifukwa, mnyamatayo anali atapita kukaphunzira, ndipo zoonadi iye anali ndi Ph.D. yake, koma iwo anali ndi kutsimikizira kwa Mawu. Iye anali ndi kutsimikizira kwa digirii kuchokera ku koleji inayake, koma iwo anali ndi kutsimikizira kwa Mawu a Mulungu kuchokera Kumwamba, ndi Mzimu Woyera kuti uyimire kumbuyo zimene iwo ankazikamba. Inde, bwana. Ndipo Mulungu anamupatsa iye zizindikiro. Inde, bwana. Oh, momwe ine ndikumuthokozera Mulungu chifukwa cha zimenezo! Anthu a Mulungu nthawizonse amakhala ndi zimenezo.

104 Tsopano, mosakayikira, wosakhulupirira amayenera kukhala ndi Mawu a Mulungu pang'ono, kuti awapotoze Iwo mozungulira, kuwapanga Iwo kuti agwirizane ndi kachikhulupiriro, kuwapanga iwo kukhala achinyengo kwambiri. Tsopano, inu mukudziwa, bodza lalikulu kwambiri

limene linayamba lanenedwapo linali ndi Choonadi chochuluka mwa ilo. Zimenezo ndi zoona. Kumbukirani. Lirilonse... Bodza loyamba limene linanenedwapo, linali ndi Choonadi nainte-faivi peresenti, pamene Satana anamuuza Eva, mmunda wa Edeni, "Zinthu zonsezi zimene Mulungu wanena." Iye anavomereza, "Uko nkulondola." Iye anavomereza, "Uko nkulondola, chirichonse chimene Mulungu ananena. Koma," anati, "ndithudi iwe sudzafa." Ndi zimenezotu pamenepo.

105 Winawake akanakhoza kunena kuti, "Iwo anali ku kachisi, kumtunda kuno usiku *wakuti-wakuti*." Inde. "Anthu onse anasonkhana mkati." Inde. "Iwo anayimba nyimbo." Inde. "Ndipo mtumikiyo anayankhula." Inde. Uko nkulondola. "Ndiyeno inu mukudziwa chiyani? Iwo anadutsitsa botolo pozungulira, ndipo onse a iwo analedzera." Zolakwika. Mukuona?

106 Basi Mzimu unagwa pansi, iwo onse analedzera. Mukuona? Ndi kusiyana kochuluka chotero basi, inu mukuona, pamene iwo sanadutsitse botolo pozungulira. Koma mdalitso wauzimu wa Mulungu unagwera pa anthu. Iwo anadzandima. Iwo anagwa. Ndipo iwo anatengeka monga chomwecho. Koma ilo silinali botolo limene linachita zimenezo. Iwo unali Mzimu Woyera ukutsimikizira Mawu Ake ndi zizindikiro zikutsatira. Mukuona? Mukuona? Zonse za zimenezo zimawoneka molondola basi, koma botololo. Mukuona?

107 Tsopano, ine ndingati, kodi inu munali pamwamba apo? "Inde." Kodi anthuwo anali kumeneko? "Inde." Kodi iwo anadzandima? "Inde. Inde." Zonsezi? "Eya." Izo zonse ziri bwino koma chinthu chimodzi chimenecho.

108 Kotero umo ndi momwe wosakhulupirira, wosa-... munthu wosadziwika ndi Mulungu, iye adzati, "Oh, ine ndimakhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu. Ine ndimakhulupirira kuti Mulungu ndi Atate wa Yesu Khristu. Ine ndimakhulupirira zinthu zina zonsezi." Mukuona? Koma pamene izo zifika ku gawo lina *Ili*, "Oh, *Ilo* ndi la tsiku lina," Mukuona? Apo pali bodza la izo. Uko nkulondola. Iye akuyesetsa kuti apotoze pang'ono Mawu olondola, kuti awapange iwo kukhala onyenga kwa anthu.

109 Koma chiyani? Yesu anapanga chinthucho kumveka bwino. Iye anati, "Zizindikiro izi zidzatsimikizira Uthenga umene Ine ndawutumiza." Inde, bwana.

110 Ine ndinakhalapo mlaliki wa Baptisti kamodzi, ndimawakonda anthu a Baptisti panobe. Koma ine ndinapeza chinthu china ichi. Mukuona? Tsopano, izo siziri—izo siziri ndendende, a—mpingo wa Chipentekoste, ine sindikunena kuti ndi wangwiro basi, mulibe kanthu mwa iwo, koma ndi wopambana umene ife tiri nawo, kotero tiyeni tikhale basi

ndi iwo. Ndizo zonse. Iwo amakhulupirira. Ena a iwo mwina sangakhale ndi chikhulupiriro chokwanira.

111 Ine ndiri ndi iwo kumene, ndiribe chikhulupiriro chokwanira kuti ndiwapangitse Mawu onse kukwaniritsidwa. Koma ine sindidzayima konse mu njira ya winawake amene ali ndi chikhulupiriro chokwanira kuti awapangitse Iwo kukwaniritsidwa. Ine sindidzabisala konse kuseri kwa kusakhulupirira, ponena kuti izo sizingachitike. Ngati munthuyo angathe kutenga Mawu a Mulungu ndi kuwatsimikizira Iwo ndi mphamvu ya Mulungu, ine ndimati, "Ulemelero kwa Mulungu! Ambuye, ndikwezeni ine mmwamba ndipo mundirole ine ndiyime, mwa chikhulupiriro, pa dziko la mmwambamwamba." Inde. Ine ndithudi ndidzakhala ndi zimenezo.

112 Iwo amangochita pang'ono pokha, kuti zigwirizane ndi kachikhulupiriro kawo. Koma wantchito wa Mulungu amakhala ndi chizindikiro Chake, ndendende.

113 Chipangano Chakale, kunkakhala kuli munthu, pamene ena a iwo akalephera kulemba dzina lawo, kotero iwo amakhala ndi chisindikizo, ndipo icho chimakhala chizindikiro. Iwo ankasindikiza icho, monga *chomwecho*. Izo zimakhala kuti zatsirizika. Chisindikizo ndi ntchito yotsirizidwa.

114 Aefeso 4:30 amati, "Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo mpaka Tsiku la Chiwombolo chanu." Ndi kusindikiza, ntchito yotsirizidwa; kuti Mulungu wakuwonani inu, wazindikira chikhulupiriro chanu chimene inu mumadzinenera mwa Iye, anatsanulira Mzimu Woyera, ndipo anakusindikizani inu mpaka Tsiku la Chiwombolo chanu. Icho ndi chizindikiro chakuti Mulungu anakupatsani inu Mzimu Woyera, uko nkulondola, ndipo watsimikizira chikhulupiriro chimene inu munali nacho mwa Iye, ndipo akupereka chitsimikiziro cha izo pokupatsani inu Mzimu Woyera.

115 Ndipo ngati inu muli ndi Mzimu Woyera, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Ndendende.

116 Ngati iye akukana, munthu uyu amene akupita mozungulira, nkumati, "Tsopano, inu musamawamvetsere anthu amenewo. Inu munali kumusi ku kachisi usiku wina?"

"Inde. Uh-huh."

117 "Chabwino, ife ndi a *Wakuti-ndi-wakuti*. Izo si kanthu koma mulu chabe wa zinyalala."

118 Kodi inu mumadziwa kuti Paulo ananena kwa Agrippa, "Mu njira imene imatchedwa 'mpatuko,' umo ndi momwe ine ndimamupembedzera Mulungu wa makolo athu"? Inu mukudziwa chimene mpatuko uli? [M'bale akuti, "Kupenga."—Mkonzi]. Eya. Uko nkulondola. Kodi iwo sananene kwa

Yesu, "Tsopano ife tikudziwa kuti Ndinu wopenga"? *Kupenga* kumatanthauza "misala." Mukuona?

119 "Njira imene imawoneka yamisala." Chifukwa inu mwadutsa kuchokera ku imfa mwapita ku Moyo. Inu simulinso a mdziko, koma inu munayikidwa pambali kuchoka kwa dziko lapansi. Mukuona? Ndipo kotero malingaliro anu ndi auzimu, ndipo inu mumaganiza za zinthu Zakumwamba ndipo osati zinthu zimene zikuchitika kuno ku dziko lapansi. Zokonda zanu ziri pa zinthu Zakumwamba.

120 Tsopano, ngati munthu uyu akukana kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

121 Tsopano penyani zimenezo. Iwe umawamva iwo akuti, "Oh, Iye ali yemweyo." Kodi Iye ali yemweyo? Kodi Iye ali yemweyo? "Chabwino," iwo amati, "Iye ali yemweyo, mwanjira inayake." Njira yake iti? Mukuona? Njira yake iti? "Chabwino, ine—ine sindi . . . Ine ndimakhulupirira kuti Iye akupulumutsabe." Mukuona? Nanga bwanji kuchiritsa? "Oh, ayi. Iye samachita zimenezo."

122 Tsopano, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, iwo anati, "Iye akhoza kuchiritsa, koma Iye sangapulumutse." Tsopano iwo akuti, "Iye akhoza kupulumutsa, koma Iye sangachize." Mwaona, ndi mdierekezi basi, akutenga mbali nkuzisinthanitsa.

123 Koma ngati Iye ali Yesu Khristu, nkomwe, Mmodzi wodzozedwayo, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Mchiritsi yemweyo, yemweyo.

124 Si inuyo amene mumachita zozizwitsa. Ayi. Iwo amafuna kunena kuti, "Ndiroleni ine ndikuwoneni inu mukuchita *izi*." Tsopano, Mulungu sananene konse kuti ine ndizichita izo. Iye anazichita kale zimenezo. Chinthu chokhacho choti ine ndichite ndi kutenga Mawu Ake ndi kugwiritsitsa kwa Iwo, ndipo Iye adzawakwaniritsa iwo. Uko nkulondola. Ndizo ndendende. Si inuyo ayi. Ndi Mulungu amene ali mwa inu.

125 Monga Yesu anati, "Si Ine amene ndikuchita ntchitozi; ndi Atate Anga amene akukhala mwa Ine. Iwo akuchita ntchitoyo. Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha; koma chimene Iye awawona Atate akuchita, chimenecho amachitanso Mwanayo." Iye ankayang'ana poyamba, kuti awone masomphenya, chimene Atate amuuza Iye. Yohane Woyera, ine ndikukhulupirira, 5:19, inu muwerenga zimenezo, 5:19. Inde. Ngati inu mungawerenge, Iye anati, "Chimene Atate andiwonetsera Ine kuti ndichite, chimenecho Inenso ndimachichita."

126 Tsopano ife tikupeza, ndiye, kuti ngati ife—ngati ife . . . ngati iye akukana kuti Yesu Khristu siali yemweyo.

127 Pali chinthu chimodzi chokha chimene Iye sangakhale, chimene Iye angakhoze kukhala wosiyana, ndicho, logwirika,

m'thupi logwirika. Mukuona? Tsopano, mu logwirika, thupi logwirika, Mulungu analiwukitsa ilo kuchokera mmanda, pa tsiku lachitatu, ndipo ilo likukhala ku dzanja lamanja la ufumu Wake Mmwamba, pa . . . pa Mpandowachifumu Wake. Yesu anagonjetsa, anakatenga Mpandowachifumu wa Mulungu. Ife amene tigonjetsa tidzakakhala ndi Iye pa Mpandowachifumu Wake, chifukwa Mpandowachifumu Wake ndi mpandowachifumu wa Davide, pamene Iye ati adzalamulire pano pa dziko lapansi. Ndipo tsopano pa dzanja lamanja la Mulungu, dzanja lamanja la mphamvu Yake ndi ufumu, Yesu akulamulira.

128 Tsopano, Mmenemo, Iye ndi Wansembe Wamkulu kuti apange kupembedzera pa kuvomereza kwathu, pamene ife tivomereza Mawu Ake, kuwakhulupirira Iwo mu mtima mwathu, kuwalandira Iwo mmenemo, ndipo osawabweza mmbuyo, koma kukhulupirira ndendende kuti izo zichitika. Mbewu yoona ya Abrahamu idzagwiritsitsabe ku Mawu amenewo. Ziribe kanthu kuti izo zitenga nthawi yotalika chotani, Iye adzakwaniritsa izo. Mulibe funde mmenemo, mulimonse. Iye adzakwaniritsa izo. Uko nkulondola.

129 Tsopano, wabodza adzati, "Ayi. Izo, izo siziri chomwecho." Ndiyeno pamene iwo akukana utumiki *Uwu*, izo zikusonyeza kuti iwo sangakhoze kuwonetsa . . . iwo . . . utumiki wawo wasindikizidwa. Iwo sangathe kukuwonetsani inu, chifukwa iwo akukana. Ngati . . .

130 Ndipo ngati—wogwira ntchito, ndingati, "Chabwino, apa, ndine wapolisi waku United States. Ndikudziwa kuti ndine wapolisi, ndipo *apa* pali lamulo limene limati wapolisi akuyenera kunyamula zomuyenereza izi, zosindikizidwa ndi chisindikizo cha United States."

131 Inu mukuti, "Chabwino, izo zinali za nthawi ina imene inapita. Ife sitikusowa kuti tikhale ndi zimenezo lero." Iye ndi wabodza. Ndizo zonse zomwe ziripo kwa izo. Iye siwolondola. Iye sanatumidwe. Iye si wotumidwa.

132 Ndipo munthu aliyense amene ati adzakane, kuti Yesu Khristu siali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; munthu aliyense amene ati adzakane "zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira," akuyesetsa kudutsa ndi mtundu wina wa pepala la kudzozedwa popanda chisindikizo cha kutumidwa. Uko nkulondola ndendende, tsopano. Ndithudi ndi choonadi. Sangakhoze kutumidwa ndi Mulungu, chifukwa iye akukana chisindikizo chomwecho, kuti, kutsimikizira kumene kwa utumikiwo kumene iye akuyenera kukhala nako.

Ngati wapolisi atati, "Inu simukusowa kukhala ndi chisindikizo chimenecho."

133 Inu muli nacho icho, inueni. "Ndi ichi *apa*, mu bukhu limene limati inu mukuyenera kukhala ndi chisindikizo chimenecho.

*Apa,* ziripo m'malamulo a United States, zimanena kuti wapolisi akuyenera kunyamula chisindikizo ichi." Ndipo ngati iye alibe chisindikizo chimenecho, iye mwamtheradi si wapolisi. Inu musamulandire iye, chifukwa iye si wapolisi, chifukwa lamulo la bukhulo limati iye akuyenera kunyamula chisindikizo chimenecho.

134 Yesu anati, "Zizindikiro izi *zidza*watsatira iwo. *Zidza*watsatira iwo!" Osati, "Zikuyenera kutero; mwinamwake; zina za izo, izo zidzatero." Ilo linati, "Izo zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Icho ndicho chitsimikiziro cha utumiki, kuti iwo anali atatumidwa. Ameni. Ine ndikuzikonda zimenezo. Izo zimangondichitira ine ubwino kudziwa zimenezo. Inde, bwana. Kotero ine ndikudziwa kuti umenewo ndi utumiki umene unabwera mu mtima mwanga, chisindikizo cha Mzimu Woyera. Uko nkulondola.

135 Ine ndikudziwa, wokhulupirira aliyense amene ali kwenikweni wokhulupirira, iye amamuwona munthu amene amakana mphamvu yakeyo: Baibulo linati, "Mmasiku otsiriza iwo akanadzakhala ndi mawonekedwe aumulungu, ndipo akanadzakana mphamvu yakeyo. Kwa oterowo chokaniko. Musalandire zimenezo, nkomwe." Kulondola. Iwo adzakhala ndi matchalitchi akuluakulu ndi zipembedzo zabwino, ndi ulemelero waukulu, ndi kukongola kwakukulu, ndi zina zotero monga choncho.

136 Taonani, kuno, usiku wina, kumusi kuno mu Phoenix, gulu la atsikana aang'ono amenewo, anyamata kunja uko, akupanga gwedemula watsopano uyu, chirichonse chimene inu mumazitcha izo kunja uko, ndipo anadzazidwa kwambiri mu mzimu wa zimenezo mpaka iwo anali kunja mmisewu. Apolisi anachita kuwanyamula iwo. Atakopedwa kwambiri pansi pa mphamvu ya mdierekezi, inde, ndiyeno izo ndi zotchuka.

137 Koma mulole munthu avine mu Mzimu nthawi yina, pansi pa mphamvu ya Mzimu Woyera! Uko nkulondola. Ndi zimenezotu. "Zizindikiro za Mulungu zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Eya.

138 Sangathe—sangathe kunena kuti iye ndi wotumidwa kuchokera kwa Mulungu, ndipo kenako nkukana utumiki Wake. Tiyeni tiyang'ane pa ena a iwo amene Mulungu anawatuma, tipeze ngati Iye nthawizonse ankawazindikiritsa okhulupirira Ake. Tsopano penyani.

139 Tiyeni timutenge Mose. Mose anali ndi kuyitana mmoyo wake, izo nzoona, koma iye anali asanatumidwe nkomwe. Iye ankaganiza kuti iye anatumidwa, ndipo taonani kulephera komwe iye anapanga. Koma pamene Mulungu anamutuma iye kuchokera pa chitsamba chonyeka...Pamene iye anali uko mu kukhalapo kwa seminare ya Farao, iye anatuluka

ndi zomuyenereza zake. Izo sizinagwire ntchito. Mulungu sakanazizindikira izo.

140 Taonani, iye anapita kumeneko ndipo anakapha munthu mmodzi wopanda kutumidwa kuti akachite zimenezo, ndipo iye anachita kuthawa kuchoka mu Igupto. Ndipo iye anapita kumusi uko ndipo anakamiza ankhondo onse a Igupto, ali ndi kutumidwa koti achite zimenezo, ndipo palibe chimene chinanenedwa za izo. Uko ndiko kusiyana kwake. Kupha munthu mmodzi ndipo anachita kuthawa. Oh, ndi mawonekedwe oyipa bwanji amene iye analimo, chifukwa iye anachita izo wopanda kutumidwa. Koma iye anapita kumeneko ali ndi kutumidwa, ndipo anakamiza ankhondo onse, anakatengera ulemelero kwa Mulungu chifukwa cha Iye. Mukuona?

141 Momwe Mulungu amawapangitsira anthu kuti azichita moseketsa! Bambo wachikulire ameneyo, wolemekezeka tsopano, anabwera kuchokera kumeneko ndi mitundu yonse ya madigirii aku koleji. Koma, ndipo, oh, iye sakanaganiza za izo, apa ali wa usinkhu wa zaka eyite. Ndipo mmawa wotsatira, apa iye akupita cha ku Igupto, ali ndi mkazi wake atakhala pa chishalo cha bulu, ali ndi mwana wake mchiuno mwake, akupita motsatira, ndevu zazikulu zakale zikulendewera monga *choncho,* ndi ndodo yokhota mdzanja lake.

“Kodi iwe ukupita kuti, Mose?”

142 “Ndikupita ku Igupto, kuti ndikalande.” Kuwukira kwa munthu-mmodzi. Bwanji? Chinthu chake ndi chakuti, iye anachita izo. Kulondola. Monga munthu mmodzi akupita kuti akatenge Russia yense. Icho chinali chiyani? Iye anathawa . . . Pamene iye anali ofesala wa udindo waukulu, ofesala wapamwamba kwambiri amene analipo, wotsatira kwa Farao mu Igupto, iye anathawa kuchoka ku Igupto chifukwa iye analibe kutumidwa koti akawawombole ana a Israeli. Koma kenako iye anabwerera, munthu mmodzi motsutsana ndi chinthu chonsecho, ali ndi kutumidwako, ndipo anakachita zimenezo. Chifukwa chiyani? Iye anali ndi kutumidwa, ndipo iye anali ndi kutsimikizira kwa iko. Iye ankakhoza kutsimikizira kuti Mulungu anali atamutuma iye. Ameni.

“Kodi iwe ukachita izo ndi chiyani, Mose?”

“Ndodo yakale yokhota iyi imene ndiri nayo mdzanja langa.”

“Ukukachita chiyani?”

“Uku ndi kutumidwa kwanga.”

“Chiyani?”

143 “Mulungu wandipatsa ine zizindikiro ziwiri zoti ndikazichite pamaso pawo. Ndi zimenezotu. Iye anandiuza ine kuti ndipite ndikachite izi. Anati, ‘Zizindikiro izi zidzawatsatira,’ ngati nditi ndipite kumusi uko. ‘Ukayiponyere

iyo pansi pamaso pa Farao, ukawone chimene chiti chikachitike. Iyo ikasanduka njoka. Ndiye ukati, "PAKUTI ATERO AMBUYE, Farao, asiye anthu Anga azipita."""

144 Mose anapita kumeneko ndipo anakaiponyera iyo pansi. Amatsenga anabwerapo, anadzachita chinthu chomwecho. Kenako Mulungu anatsimikizira utumiki wake. Njoka yake inadya zina zonsezo.

145 Kodi inu munayamba mwaganizirapo, "Kodi njoka zimenezo zinapita kuti?" Kutiko? Chinachitika ndi chiyani kwa ndodo zimenezo? Izo zonse zinali mu ndodo imodzi. Mukuona? Iyo inazidya izo, njoka ya Mose. Chifukwa, icho chinali chiyani? Chitsimikiziro. Ameni. Aleluya! Iye anali ndi kutsimikizira kwa utumiki wake. Iye anawuchita iwo. Iye anawatulutsa anawo, ndipo Nyanja Yofiira inali mu njira yake ndipo inapereka njira.

146 Chifukwa chiyani? Iye anali ndi kutumidwa ndi kutsimikizira kwa iko. Mulungu anali ndi iye, ndipo anachita zizindikiro ndi zodabwitsa.

147 Koma, pamene, ngati munthu watumidwa ndi Mulungu wa chauzimu, mphamvu ya chauzimu ya Mulungu idzakhala ndi kutumidwa kwa chauzimu kumeneko. Osati zimene inu mumaphunzira mu Ph.D. ndi LL.D. ndi algebra, ndi zinthu zonsezo. Izo zimatsimikizira galamala yanu yabwino ndi kuyankhula pa guwa pamene inu munena kuti, "Ah-meni" ngati ng'ombe. Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Koma pamene inu muli ndi kutsimikizira kwa utumiki wa Mulungu, woperekedwa kwa inu ndi Mzimu Woyera, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Mundikhululukire chifukwa cha mawu amenewo.

148 Kutsimikizira. Mulungu anatsimikizira, chifukwa Iye anali Mulungu wa chauzimu, anapereka mphamvu ya chauzimu, kwa chiwombolo chauzimu. Ine ndikukhulupirira zimenezo.

149 Mulungu lero sawawombola anthu Ake ndi maphunziro. Iye sanalonjezepo konse kuti akanadzachita zimenezo. Iye sawawombola iwo ndi maphunziro azafioloje. Iye sanalonjezepo konse kuti akanadzachita izo. Iye sawawombola iwo ndi sayansi. Iye sanalonjezepo konse kuti akanadzachita zimenezo. Iye sawawombola iwo mwa chipembedzo. Iye sanalonjezepo konse kuti akanadzachita zimenezo. Koma Iye adzawawombola iwo mwa mphamvu, mphamvu ya chauzimu, ya kusintha miyoyo yawo ndi kuwawumba iwo kukhala ana a Mulungu. Ameni.

150 Mose anali ndi utumiki. Iye anali ndi zizindikiro zoti zitsimikizire utumiki wake.

Tsopano, Yesu, mwanjira yomweyo, anati, "Zizindikiro izi!"

151 Mose anati, "Kodi ine ndingawauze iwo chiyani? Ine ndikawauza bwanji iwo kuti Mulungu wa makolo awo wanditumа?"

Anati, "Iwe uli ndi chiyani mdzanja lako?"

Anati, "Ndodo."

152 Anati, "Iponye iyo pansi. Ika dzanja lako mu chifuwa chako, tuluka. Ukalalikire machiritso Auzimu kwa iwo." Icho ndi chitsimikiziro. Zedi. "Ine ndikupatsa iwe zizindikiro ziwiri."

153 Tsopano, Mulungu yemweyo sangasinthe. Pamene Iye anawutumiza Mpingo Wake kumeneko, kuti ukawombole anthu kuchoka mu ukapolo wa gehena uwu wa ku Igupto umene zinthu zonsezi zimene zawafikitsamo anthu lero, Iye anati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Musakachite mantha kukawayala Mawu amenewo kunja uko, chifukwa iwo ndi Choonadi. Iwo ndi Mawu a Mulungu. Musakalole kuti mdierekezi akawafotokoze Iwo molakwika kwa inu; chifukwa izo si zolondola. Iye amasunga Mawu Ake. Tsopano, ine ndimakhulupirira zimenezo ndi zonse zimene ziri mwa ine.

154 Eliya anatumizidwa kumeneko. Ine ndikukhoza kumuwona iye mmawa umenewo. Ine ndikuganiza kuti iye ndi Yezebeli anali ndi zotsemphana pang'ono. Koma apa iye anali tsiku limenelo akubwera kumeneko, munthu wamng'ono wokalamba wa mutu wadazi, ndi ndevu zikulendewera pansi, akubwera kumatsika mmawa umenewo, kumusi pa msewu uja waku Samariya. Maso amenewo akuyang'ana mmwamba momwe; kumwetulira kuli pa nkhope yake. Ndodo yakale ija ikumenya pa msewu. Koma, m'bale, iye anali ndi "PAKUTI ATERO AMBUYE."

155 "PAKUTI ATERO AMBUYE." Iye anayenda mpaka pa nkhope pomwe pa purezidenti kapena pa mfumu, anati, "Sipadzakhala nkomwe mame ati adzabwere kuchokera kumwamba mpaka ine nditawaitanitsanso iwo." Icho chinali chiyani? Iye anali ndi kutumidwa. Kodi mvula inagwa tsiku lotsatira? Ayi. Iye anali ndi kutsimikizira kwa izo. Mukuona?

156 Anati, "Pita uko, Eliya, ndipo ukakhale pansi. Ine ndakulamulira iwe kuti ukakhale ndi okunyamulira akatundu ena ndi antchito kuti abwere azikakudyetsa iwe." Kotero makungubwe ankamudyetsa iye.

157 Ndipo pamene iye anali adakali pamwamba pa phiri paja tsiku lina, "Oh," mfumu inati, "palibe kanthu kwa munthu ameneyo. Ine nditumiza amuna fifite. Ine sindikukhulupirira kuti iye ali kanthu koma wotentheka wachikulire. Kodi ife sitinamudziwe iye cha kuno, akuyankhula za Yezebeli, mkazi wanga, zokhudza kupaka penti ndi chirichonse monga zimenezo, kumayankhula za makhalidwe amakono onsewa?"

158 Ndi kumakhala moyo motsatira dona woyamba ngati chitsanzo, monga ambiri a ife anthu Achipentekoste timachitira! Eya. Uko nkulondola. Akazi athu Achipentekoste, kametedwe kotchuka ka phanke, ndi zinthu monga zimenezo, inde, eya, kumapaka penti, zophodaphoda, kumavala akabudula. Ndipo Baibulo linati, "Ndi chonyansa pamaso pa Mulungu." Inu

mungachite bwanji zimenezo? Uko nkulondola. Bwanji, inu mukudziwa, ngati inu mumadzinenera, mlongo, inu, chinachake chagwa, ngati inu mungakhoze kukhala ndi tsitsi lodula, ndipo Baibulo limati . . .

159 Tsopano, ambiri a inu akazi Achipentekoste simumadziphodaphoda. Mulibe chirichonse m'Baibulo chokhudza zimenezo. Koma ndiye inu mumadula tsitsi lanu. Ndipo Baibulo linanena, kuti, "Mkazi amene amadula tsitsi lake ndi wosalemekezeka." Uko nkulondola.

160 Ndipo inu mumavala akabudula, kapena zazing'ono zakale izi . . . Ndi a . . . Mukuona? Chirichonse chimene icho chiri, chimawoneka ngati chovala cha mwamuna. Ndipo Baibulo linanena, kuti, mkazi aliyense amene adzavale zovala zonga zimenezo, "Ndi chonyansa pamaso pa Mulungu." Mwa kuyankhula kwina, "Izo—izo zimanunkha moyipa, kwa Mulungu. Izo zimawoneka moyipa." Ndiyeno ngati inu muli ndi Mzimu Woyera mwa inu, chimene ndi Mulungu, inu mungamavale bwanji zimenezo ndipo nkumadzinenerabe kuti muli ndi Mzimu Woyera? Bwanji, moyo wanu womwe umatsimikizira kuti pali chinachake cholakwika ndi inu. Uko nkulondola.

161 Ine ndikudziwa kuti zimenezo zikuwotcha, koma ine—ine ndikukuuzani inu lomwe liri vuto usikuuno. Ife tikusowa kuwotcha kwina kochuluka ndi kumene iwo akukusowa, kukwapulidwa kwina kochuluka. Uko nkulondola. Ndiro limene liri vuto, ife talekelera pa zinthu zimenezo. M'bale, ndiroleni ine ndikuuzeni inu, inu mukuyenera kuti muphunzire ma ABC anu inu musanapite patali paliponse, inu mukuona, uko nkulondola ndendende, kuti nthawizonse muzikhulupirira kuti Mawu a Mulungu ndi owona. Ziribe kanthu chimene icho chiri, muzingofanizitsa ndi Iwo. Inde, bwana.

162 Eliya atakhala pamwamba pa phiri apo, ndipo Mulungu anati, "Tsopano, iwe susokonezeka." Anati, "Ine ndikutuma iwe kumeneko mpaka anthu amenewo atalapa."

163 "Oh," Ahabu anati, "ife sitikusowa kuchita kulapa kulikonse. Wotentheka wachikulire ameneyo, iye sakudziwa chimene iye akuyankhula. Iye ndi mmodzi wa oyera odzigudubuza akale amenewo. Ife basi . . . Ndipatseni ine amuna fifite a amuna osankhidwa. 'Pitani kumeneko ndipo mukamubweretse wotentheka wachikulire ameneyo.'"

164 Ine ndikutha kumuwona ofesala wotumidwayo akuti, "Inde, bwana. Ine ndiri ndi kutuma kwanu, bwana. Ine ndimubweretsa iye."

165 Apa iye akubwera, akuguba, a—chitsulo chikumenya pansi, malupanga aakulu awa ndi mikondo, ndipo amuna fifite a kusankha kwa alonda a Ahabu anabwera akuyenda chokwera phiri monga choncho.

Apo panakhala Eliya pamwamba apo mu dzuwa lotentha, akuyang'ana pozungulira monga *choncho*.

166 Iwo anati, "Hei! Ife tikukutsatira iwe, mnyamata. Ife tiri ndi zoyenereza zathu apa. Ndife alonda a Ahabu. Ife tikukufuna iwe. Ife tikutenga iwe tipite nawe."

167 Iye anadzuka, anati, "Inde, ine ndiri ndi zoyenereza zina, nanenso. Ngati ine ndiri munthu wa Mulungu, mulole moto ugwe kuchokera kumwamba." Icho chinali chiyani? Icho chinali chitsimikiziro. Inde, bwana.

168 Pa Phiri la Karimeli, pamene iye anali ndi chiwonetsero pakati pa milungu yabodza ndi Mulungu woona. Iye anayika nsembeyo pamenepo, anayenda kupita kumeneko, ndipo anati, "Ambuye Mulungu wa Abrahamu, Isaki, ndi Israeli, mulole izo zidziwike lero kuti Inu ndi Mulungu mu Israeli, ndipo ine ndi wantchito Wanu, ndipo ine ndachita zonsezi mwa kutuma Kwanu."

169 "Ndalalikira Mawu," mwa kutuma Kwanu, Ambuye, "ku dziko lonse, kwa cholengedwa chirichonse. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Kutuma kwanu.

170 "Tsopano, Ambuye, mulole chidziwike kuti Inu munandiuza ine kuti ndichite izi. Inu munandituma ine kuti ndidzachite izi, tsopano tsimikizirani izo, Ambuye." Ndipo pafupifupi nthawi imeneyo, moto unagwa kuchokera kumwamba. Icho chinali chitsimikiziro cha zimenezo. Iye anali ndi Mawu. Mukuona?

171 Mulungu nthawizonse amatsimikizira Mawu Ake. Iye— Iye amapereka chitsimikiziro cha Mawu Ake. Tsopano, ife tikudziwa kuti izo ndi zoona. Oh, ndi nthawi zingati zimene . . . Ife tiri ndi anthu osiyanasiyana pano amene tingakhoze kumapitirirabe nawo mpaka mmusi. Koma kuti tisunge nthawi . . .

172 Yesu, pamene Iye anabwera pa dziko lapansi, ndipo iwo anati, "Iye, pokhala Munthu, akudzipanga Yekha kukhala Mulungu? Oh, mai! Chabwino, ife tikudziwa chimene Iye anali. Iye anabadwa mwapathengo. Bwanji, Iye siali nkomwe . . . Ife timawadziwa amayi Ake, Maria, ndi Yosefe. Iwo anali ndi mwana ameneyo asa- . . . "

173 Yesu anati, "Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine. Inu simukukhulupirira kuti Ine ndi Mesiya? Ntchito zimene Ine ndikuzichita zikutsimikizira chimene Ine ndikudzinenera. Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musakhulupirire izo. Koma ngati Ine ndikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye inu mukhulupirire ntchitozo, ngakhale kuti inu simungandikhulupirire Ine." Chimenecho chinali chitsimikiziro. Kodi izo zinawayenera chotani iwo? Zedi. Anati . . .

174 Mulungu, amene Mulungu amamutuma, Mulungu amamutetezera. Mulungu amatsimikizira Mawu. Ngati Mulungu amutuma kazembe kwinakwake, kuti akachite chinachake, Iye akuyenera kuti ayime kumbuyo kwa kutuma kumeneko. Ndizo ndendende kulondola.

175 Iye anati, "Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye inu musati—inu musandikhulupirire Ine, koma," anati, "ntchito zomwezo zimene Ine ndikuzichita zikutsimikizira kutuma Kwanga." Ameni. Izo ndithudi zinawamenya iwo. Sichoncho izo? "Ntchito zimene Ine ndikuzichita." Eya. Inde, bwana. "Ngati inu simutero, ngati inu simungakhulupirire kuti ine ndinatumizidwa ndi Mulungu, ndiye chinthu choti inu muchite ndi kukhulupirira zimenezo, ntchito zimene Ine ndikuchita, kapena, ndiroleni ine ndikuwoneni inu mukuchita ntchito zomwezo," ndi zimenezotu, "ngati inu simukundikhulupirira Ine." Izo . . . Oh, mayi!

Analipo ena a iwo anamukhulupirira Iye.

176 Pamene mkazi wapa chitsime anawona chizindikiro Chake cha Umesiya, iye anati, "Ife tikudziwa kuti Mesiya amachita zimenezo." Anapita ndipo anakawauza anthu, anati, "Bwerani, mudzawone Yemwe ine ndamupeza, Munthu amene wandiuza ine zinsinsi zomwe za mtima wanga. Kodi ameneyo si Mesiya?"

177 Nataniele wakale, pamene iye anabwerera ndi Filipo, ndipo Yesu . . . anayenda kupita mu Kukhalapo kwa Yesu, ndipo Yesu anati, "Taonani m'Israeli amene mwa iye mulibe chinyengo."

178 Tsopano, iye anali munthu wophunzitsidwa, chifukwa iye ankawadziwa Mawu. Iye ankadziwa kuti Mesiya akanadzakhala Mulungu-mneneri. Kotero iwo ankadziwa kuti Mose anali atanena zimenezo. "Ambuye Mulungu wanu adzawutsa mneneri." Iye ankadziwanso, kuti Mulungu anati, "Ngati patakhala mmodzi pakati panu, yemwe ali wauzimu kapena mneneri, Ine, Ambuye, ndidzamutsimikizira iye. Ine ndidza . . . Chimene iye anena, chikachitika, ndiye mukhulupirire izo." Mukuona? Iwo ankafuna kuti afufuze ngati Iye anali. Iwo ankadziwa kuti pankayenera kukhala mneneri adzawuke pafupifupi nthawi imeneyo, ndipo iwo ankafuna kudziwa Yemwe Iye anali.

179 Kotero iye anayenda mpaka pamaso pa Filipo, ndipo Filipo anamuuza iye choti achite. Kapena, Filipo anamutengera iye mu Kukhalapo kwa Yesu, kani.

180 Ndipo pamene iye anayenda mpaka pamaso pa Yesu, Yesu anati, "Taonani m'Israeli mwa yemwe mulibe chinyengo."

"Inu munandidziwa bwanji ine, Rabbi?"

181 Anati, "Filipo asanakuyitane iwe, pamene iwe unali pansi pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe."

182 Iye anati, “Rabbi, Inu ndi Mwana wa Mulungu.” Apo panali zomuyenereza Zake.

183 Mkazi pa chitsime, pamene Iye anamupeza iye atayima pamenepo pa chitsime, Iye anati, “Ndibweretsere Ine akumwa.”

184 Iye anati, “Si chamwambo wake. Inu mukuchoka mu wathu—wathu—mwambo wathu kuno. Ife tiri ndi kusankhana. Ife Ayuda ndi Asamariya tiribe chiyanjano kwa wina ndi mzake. Inu pokhala mwamuna, Myuda, ndipo ine mkazi wa Chisamariya, izo zikutheka bwanji kuti Inu mundifunse ine kuti ndikuchitireni Inu chifundo, kukubweretserani Inu akumwa?”

185 Iye anati, “Mkazi, ngati iwe ukanadziwa Yemwe iwe ukuyankhulana naye, iwe ukanandipempha Ine akumwa.”

186 Ndipo iye anati, “Bwanji, chitsimechi ndi chakuya. Inu mulibe kanthu koti mutungire.”

Iye anati, “Madzi amene Ine ndimapereka sali mu chitsime chimenecho.”

187 Mopitirira, anapitirira, kukambiranako kunapitirira kwa kanthawi, mwaona, mpaka Iye, chimene Iye ankayesera kuti achite: Ankafuna kuti akhudze mzimu wake, kenako Iye anapeza pomwe vuto lake linali. Anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo ubwere naye kuno.” Ankafuna kuti iye, adziwe Yemwe Iye anali. Anati, “Pita, ukamutenge mwamuna wako ndipo mubwere kuno.”

Iye anati, “Ine ndiribe mwamuna.”

188 Anati, “Izo nzoona. Iwe wakhala nawo faivi, ndipo amene iwe ukukhala naye tsopano si mwamuna wako.”

189 Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi mneneri.” Anati, “Ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera Iye adzachita zimenezo.”

Iye anati, “Ine ndi Iye amene ndikuyankhula ndi iwe.”

190 Iye anabwera mu mzindawo. Izo zinatsimikiziridwa kwa iye. Iye anapita mu mzinda ndipo anati, “Bwerani, mudzamuwone Mwamuna Amene wandiuza ine zinthu zimene ine ndazichita. Kodi uyu si Mesiya amene? Kodi icho si chitsimikiziro chakuti Iye ali?”

191 Yesu anati, “Ntchito zomwezo zimene Ine ndikuzichita zikutsimikizira utumiki Wanga.” Uko nkulondola. Mulungu anamutuma Iye. Iye anali woti adzakhale Mneneri ameneyo.

192 Inu mukudziwa, iwo ananena kwa Yohane, “Kodi iwe ndi Eliya? Kodi—kodi ndiwe mmodzi wa aneneri? Kodi iwe ndi Mneneri ameneyo amene anali woti adzabwere?”

193 Yohane anati, “Ine sindiri. Koma Iye wayima pakati panu, penapake. Iye adzazitsimikizira Yekha pamene Iye adzabwera, chifukwa Mulungu adzamutsimikizira Iye.” Ndiko kulondola ndendende. Ngati munthu watumidwa ndi Mulungu, Mulungu

ndi wokakamizika kuti amutsimikizire munthu ameneyo, ndiko kulondola ndendende, kuti iye watumizidwa. Oh, inde, chitsimikiziro.

194 Munthu uja amene anabadwa wakhungu, anali ndi umboni wokhutitsa kwambiri wakuti Iye anali Mesiya. Tsopano, munthu wosawukayo, iye sana—iye sana . . . Pamene azafioloje onsewo anamugwira iye mu unyinji kumtunda uko, ndipo anati, "Kuti, ife tikudziwa kuti iwe unabadwa wakhungu." Anati, "Ife tikudziwa kuti—kuti iwe unalibe mipira yammaso, ngakhale mmabowo." Anati, "Ife tikudziwa kuti iwe unabadwa wakhungu." Iye anati, "Ndani wakuchiritsa iwe?"

195 Ndipo iye anati, "Mwamunayo anandiuza ine kuti ndachiritsidwa." Anati, "Ine ndikudziwa Iye anandichiritsa ine." Anati, "Ine—ine—ine ndikudziwa zimenezo."

196 Anati, "Chabwino, tsopano, Mwamuna ameneyo ndi wochimwa. Ife tikudziwa kuti Iye ndi wochimwa, chifukwa Iye sanajowine bungwe lathu. Iye sanabwere mwa njira yathu. Iye samaphunzitsa chiphunzitso chathu. Iye amatsutsana ndi ife." Anati, "Ife—ife tikudziwa kuti Iye sangakhale wa Mulungu. Ife tikudziwa kuti pali chinachake cholakwika ndi Iye, chifukwa Iye sanagwirizane ndi ife." Anati, "Munthuyo ndi wochimwa."

197 Tsopano, munthu wosauka wakhungu uyu sakanakhoza kutsutsana ndi mfundoyo, iye sanali wazafioloje, iye—iye sakanakhoza kutsutsa mfundoyo. Iye anati, "Tsopano . . . " Koma iye anali ndi kutsutsa kokhutitsa kwambiri aponso. Iye anati, "Kaya Iye ndi wochimwa, kapena ayi, ine sindikudziwa. Koma ichi ndi chinthu chimodzi chimene ine ndikuchidziwa," ameni, "kuti ine ndinali wakhungu nthawi ina, ndipo tsopano ine ndikupenya."

198 Ine ndawamvapo anthu akunena kuti ili linali gulu la anthu openga. Ine ndinali ndi anthu akundiwuza ine, pamene ine ndinalandira Mzimu Woyera, kuti ine ndasokonezeka mmalingaliro anga. Chabwino, kaya izo nzoona, kapena ayi, ine sindikudziwa. Koma pali chinthu chimodzi chimene ine ndikuchidziwa: kuti ine ndinali wochimwa poyamba, ndipo ine tsopano ndapulumutsidwa. Uko nkulondola. Kuti ine ndinali wotayika poyamba, ndipo ine tsopano ndapezeka. Inu mukhoza kuzitcha izo kutentheka, chirichonse chimene inu mukufuna, koma ndi chitsimikiziro kwa ine kuti Iye akadali Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Uko nkulondola. Inde.

199 Iye—iye—iye anali ndi umboni. Iye anali nako kuyankhula kokhutitsa kwambiri kuti Iye anali . . . Iye—Iye anali . . . kuti Iye anali Mwana wa Mulungu, chifukwa Iye anali atapanga mipira ya mmaso mwa munthu amene analibe maso. Inde, bwana. Mwakuyankhula kwina, munthu wakhunguyo akanatha kunena kuti, "Ine ndakhala ndikubwera ku tchalitchi kwanu

nthawi yonseyi. Ine sindimawona chirichonse chonga icho chikuchitika kozungulira kuno. Ndiye ngati Iye analenga mipira ya mmaso, kulibeko Mlengi koma Mulungu. Kodi izo zikanakhoza kuchokera kuti? Tiyeni tikuwoneni inu mukuchita zimenezo. Tiyeni tiwone momwe inu mumachitira izo."

200 Iwo anakhala chete. Iwo akuyankhula za Mulungu wa chauzimu, Mlengi wamkulu wa miyamba ndi dziko lapansi, ndipo osatha kulenga moyo wabwino. Mukuona? Ndi zimenezotu pamenepo. Samatha kulenga kalikonse.

201 Koma apa panabwera Yesu ndipo anadzayika maso mwa munthu amene analibe maso, anabadwa wakhungu. Ine ndikukuuzani inu, zimenezo ndi zokhutitsa. Chitsimikiziro cha phala ndi kulidya ilo. Ndiko kulondola ndendende. Kotero iye anali ndi umboni wakuti Iye anali. Uko nkulondola.

202 Ine ndikulingalira za Paulo, kunja uko usiku umenewo, pamene masiku fortini ndi mausiku, ndipo opanda mwezi, nyenyezi, kapena kalikonse, uko pa nyanja imeneyo; munthu wamng'ono wosaukayo akukwakwaza maunyolo amenewo pansi pa ngalawa yakale itadzaza madzi imeneyo, ndipo iyo inali pafupi kuti imire pansi. Iwo anali atataya zakudya zonse ndi zinthu, ndipo okwerawo anali asanadye kwa masiku ambiri. Ndipo akukwakwaza maunyolo awa, akuyankhula za Yesu amene anakhalapo nthawi ina, akuyankhula za Yesu amene anapachikidwa.

203 Ine ndikulingalira asilikari amenewo ndi oyendetsa ngalawayo akuti, "Oh, kalanga, khala chete!"

204 Ankangopitirira kumawoloka, akuti, "Koma, inu mukudziwa, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse," akungoyenda pamenepo, pansi pakepo, akukwakwaza maunyolo amenewa.

205 Anati, "Tayang'anani pa munthuyo ali mu unyolo, munthuyo akupita kwa Kaisara kumeneko, akupita ku Roma, kuti akaweruzidwe. Munthuyo akuyenera kuti akafe, ndiyeno nkumayankhula za chinachake chokhudza chipembedzo. Oh, khala chete!"

206 Ndipo iwo anapitirira kumakwakwaza. Koma, usiku wina, pamene ziyembekezo zonse zinapita! Oh, mai.

207 Nthawi iliyonse mphenzi ikang'anima, funde, adierekezi teni sauzande amakhala pa nyanja zimenezo, amati, "Ife takupeza iwe tsopano, Paulo. Oh, iwe ubweza zimenezo."

208 "Ayi, bwana. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Uko nkulondola. Ine ndikudziwa kuti Iye anandiuza ine kuti ndipite ku Roma."

209 Apa iye ali, akugwedezeka, ngalawayo itatsala pang'ono kumira pansi. Tangoganizani, dzuwa, mwezi, kapena nyenyezi zinali zisanawale kwa fifitini, kapena masiku fortini. Amenewo

ndi mawonekedwe oyipa; ngalawa yakale itadzaza madzi, ndipo chinthucho chitatsala pang'ono kupita pansi, chirichonse monga choncho.

210 Iye anali atayima pansi mmbali mwa ngalawayo, usiku wina, akupemphera, mosakayika, ndipo apo panadzabwera masomphenya. Mngelo wa Ambuye anawonekera kwa iye, anati, "Usawope ayi, Sauli. Chirichonse chiri bwino."

211 Apa iye akubwera, akuthamanga, ali ndi kutumidwa, akugwedeza maunyolo amenewo, akuti, "Mukhale a akulimbika kwabwino. Mukhale ndi chikhulupiriro chabwino, pakuti Mulungu amene ine ndimamutumikira anatumiza Mngelo Wake usiku wathawu. Ine ndinawona masomphenya, ndipo Iye anandiuza ine kuti ndisachite mantha, chifukwa sipakhala moyo uti utayike pa ngalawayi. Chotero, abale, mudye chakudya pang'ono, ndipo muzingosangalala. Chirichonse chiri bwino."

212 Ine ndikuganiza kuti iwo anamverera mwachirendo kwenikweni. Koma pamene iwo anapeza kuti ngalawa yakaleyo yafika padoko kutaliko, izo zinatsimikizira kuti Paulo anali atatumidwa kuchokera kwa Mulungu ndipo ankadziwa zomwe iye ankazikamba. Mulungu anatsimikizira izo.

213 "Ngati pali mmodzi pakati panu mneneri, ndipo zimene iye anena zikachitika, ndiye mumumvere iye, chifukwa Ine ndiri ndi iye." Uko nkulondola.

214 Pamene, mbadwazo pa chilumba ichi, okhala pa chilumbawo, pamene iwo anamuwona iye akutola nkhuni, ndipo iwo anati, "Uyo akuyenera kukhala wakupha wina wowopsya, ma unyolo onsewo pa iye."

215 Paulo wamng'ono wosauka, atatsala pang'ono kuwuma, ndipo zovala zake zonse zitanyowa, anabwera cha kuno ndipo anadzatenga mulu wa nkhuni, ndipo anayamba kuziyika izo pa moto. Ndipo njoka imene inamuluma iye mdzanja ikanamupha iye, mai, mkamphindi. Paulo anayang'ana pa iyo, monga *choncho,* ndipo anati, "Mulungu, Inu munandiuza ine kuti ndimayenera kupita ku Roma panobe." Anaisasira iyo pa moto, ndipo anabwerera ndipo anakatenga nkhuni zina zowonjezera.

Anati, "Muwoneni iye agwa nkufa."

216 Maminiti pang'ono, iwo anasintha izo. Bwanji? Kutumidwa kwake kunali kutatsimikiziridwa. Iwo anati, "Iye ndi mulungu amene watsika kuchokera kumwamba." Kulondola.

217 Iye anali ndi chitsimikiziro, chifukwa Yesu anati, "Iwo adzaponda pa mitu ya njoka ndi zinkhanira, ndipo palibe chimene chiti chidzawapweteke iwo." Inde, bwana. Iye anali— iye anali ndi—umboni woti atsimikizire izo.

218 Tsopano ine ndikuyenera kuti ndifulumire, abwenzi. Ine ndingakhale pano ndi inu usiku wonse monga choncho. Koma basi zinthu zina zingapo zowonjezera.

219 Tsopano, mneneri anati, “Lidzakhalapo tsiku limene silidzatchedwa masana kapena usiku, tsiku lachimbuuzi, lachifunga, chimbuuzi, koma,” anati, “mu nthawi ya kumadzulo kudzakhala Kuwala.” Uko nkulondola.

220 Dzuwa limatuluka kummawa, ndipo limakalowa kumadzulo: d-z-u-w-a. Chitukuko chayenda kuchokera kummawa mpaka kumadzulo. Koma pamene M-w-a-n-a anawuka, Kuwala kunagwera pa anthu akummawa.

221 Tsopano ife takhalapo nalo tsiku la bungwe, zipembedzo, ndipo anthu akumuvomereza Khristu, ndipo anali ndi Kuwala kokwanira kumene iwo akanakhoza kudziwa kuti Iye anali Mulungu. Ndipo iwo ankayenda mu Kuwala, ndi zina zotero. Iwo amamanga matchalitchi, ndi makafidulo abwino, ndi masukulu, ndi zina zotero. Izo zakhala zabwino.

222 Koma, kumbukirani, izo zinalonjezedwa kuti mitambo yonse ikanadzachoka mu nthawi ya kumadzulo. Ndi nthawi ya kumadzulo tsopano. Ndipo pamene mitambo yonse ikuchoka, Mwana yemwe uja, M-w-a-n-a, amene ankawalitsa mphamvu Yake kupyolera mwa Mzimu Woyera pa anthu akummawa, watero, mu zaka fifite zapitazi, waphwanyanso mitambo ya zipembedzo ndi chirichonse, ndipo wadzatsanulira pansi Mzimu Woyera pa anthu akumadzulo. Kuti, Mwana yemweyo, Mzimu Woyera womwewo, chizindikiro chomwecho, Kuwala komweko, mphamvu yomweyo, umboni womwewo, chirichonse chomwecho chimene Icho chinali. Ndipo Uthenga walalikidwa ndi mphamvu ndi chiwonetsero, kulikonse mmayiko. Izo ndi zoona. Izo ndi zoona. Konsekonse mdziko, zizindikiro ndi zodabwitsa zikuwatsatira okhulupirira.

223 Kuno, zaka zingapo zapitazo, iwo anati, “Gulu limenelo,” anati, “bwanji, inu simudzatha konse.” Anati, “Iwo sadzatha konse kuziyika izo.” Anati, “Iwo angokhala gulu laling’ono kumusi uko mu—mu msewu kwinakwake, ali ndi chitini kwinakwake, akumenya nkhotcho ina yaying’ono.”

224 Koma, m’bale, uthenga umenewo, ndi anthu a mtima wanjala apereka nsembe chakudya cha ana awo, ndi china chirichonse, ndipo athandizira ma mishonare amenewo, mpaka iwo wapita kummawa, kumadzulo, kumpoto, kummwera. Fuko lirilonse limene inu mungapiteko, kuli moto wa chipentekoste ukuyaka ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

225 Ine ndapitako kutali kwambiri mu nkhalango, mpaka kwa anthu amene sankadziwa dzanja lamanja ndi lamanzere. Iwo sankadziwa kanthu za Mulungu koma chosemedwa china kunja uko. Uko nkulondola. Ine ndimatha kuyima pamenepo ndi kuwayika Mawu pansi chimodzimodzi basi. Ndiye Mzimu Woyera unkachita zizindikiro ndi kusonyeza, kuwauza anthu chimene iwo anali, zobisika za mmitima yawo, kuwasonyeza

iwo kuti Yesu anati, “Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita.”

226 “Munthu uyu, ine sindikudziwa dzina lake, koma ine nditchula ilo, ndipo inu mutanthawuzire ilo kwa ine.” Ine ndinkayenera kutchula mwinamwake mochuluka *chotero*, kuti nditulutse ilo monga *choncho*.

“Ameni. Uko nkulondola.” Iwo ankakhala ndi kuyang’ana.

227 Ine ndinkati, “Tsopano, Yesu anati, ‘Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita.’ Ichi chinali chizindikiro Chake cha Umesiya.”

228 Ndipo Yesu wayandikira kwambiri kuti abwere ku dziko lapansi tsopano, mpaka mphamvu Yake yayamba kuwagwira anthu, ndi kuwatsirizitsa iwo, kuwakonzekeretsa iwo kwa Mkwatibwi, kukonzekera kuti akwatulidwire mu Mkwatulo, Mpingo umene uti udzangokwanira ndendende basi, kuti udzatengedwere mmwamba. Kudzera mu mphamvu Yake, idzakokera ena onse a iwo amene ali obadwa mwatsopano, kuchoka pa dziko lapansi. Yesu akubwera.

229 Monga dzanja langa pa khoma likhoza kupanga mthunzi, mochuluka, mthunzi umenewo umakula ndi kukula ndi kukula, dzanja langa likamayandikira, ndipo pakapita kanthawi mthunziwo ndi dzanja langa zimadzakhala chimodzi.

230 Ndipo mpingo unayamba mu nthawi ya Martin Luther, pansi pa kulungamitsidwa; pansi pa Wesley, kudutsa mu kuyeretsedwa; ndipo tsopano mu ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi Achipentekoste, kubwezeretsa kwa mphatso. Ndipo kuchokera mwa anthu Achipentekoste amenewo Iye akuwakokera otsalira amenewo pamwamba *apa*, kuti amuwonetsere Yesu Khristu, adzanyezimiritse Moyo Wake chimodzimodzi basi dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndendende, pamene Kuwala kwa kumadzulo kukuwala. Ndizo ndendende.

231 Taonani, pa chizindikiro cha sayansi pomwe, ife tiri nacho icho mu Washington, DC, Lawi la Moto lomwe lija. Ndi angati anayamba akuwonapo Iko, Kuwala kumeneko? Zedi. Konsekonse. Mukuona? Mukuona? Lawi la Moto lomwelo limene linakomana ndi Paulo, pa njira yaku Damasiko. Yesu, pamene Iye anali pa dziko lapansi . . .

232 Aliyense akudziwa kuti Khristu, kuti—kuti Lawi la Moto, Mngelo wa Ambuye yemwe anabweretsa Israeli kuchokera ku Igupto, kupita mu dziko lolonjezedwa, anali Mngelo wa pangano. Aliyense akudziwa zimenezo. Ndithudi. Chabwino, ameneyo anali Khristu.

233 Chifukwa, Baibulo linanena, kuti, “Mose anasankha chitonzo cha Khristu kukhala chuma chachikulu kuposa chuma cha Igupto.” Ndipo iye anapita ndi Khristu, Iye asanasandulike thupi, ndipo iye anatsatira Kuwala kumeneko.

234 Yesu, pamene Iye anali padziko lapansi, Iye anati, “Ine ndinachokera kwa Mulungu, ndipo ine ndikupita kwa Mulungu.” Iwo anamupachika Iye. Iye anali Mpulumutsi amene anafera machimo athu, ndipo iye anamuyika Iye mmanda. Iye anawuka ndipo anakwera Mmwamba.

235 Ndipo miyezi ingapo zitachitika zimenezo, Paulo anali panjira yake akupita ku Damasiko, ndipo iye anagwetsedwa pansi ndi Kuwala. Gulu la asilikari liri ndi iye, palibe mmodzi wa iwo analiwona Ilo. Palibe aliyense wa iwo anamuwona Iye koma Paulo yekha. Koma Ilo linali—linali lenileni kwambiri kwa iye, mpaka Ilo linathimitsa maso ake. Iye anali wakhungu kwa kanthawi. Ndipo iye anayang’ana mmwamba umo, ndipo Lawi la moto lalikulu lija litapachikika patsogolo pake, ndipo Iye anati, “Saulo, Saulo, ndi chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

Iye anati, “Inu ndi Ndani, Ambuye?”

236 Iye anati, “Ndine Yesu, ndipo ndi kovuta kuti iwe uzimenyana ndi zisonga.”

237 Tsopano, Mzimu Woyera womwewo, ife tikuwupeza Iwo pakati pa anthu achipentekoste lero, Kuwala kwa kumadzulo, pansi pomwe pakati pa anthu achipentekoste. Chiyani? Kulalikira Uthenga womwewo, kupereka kutsimikizira kwa Uthenga womwewo. Zizindikiro zomwezo zimene zinkatsatira kumeneko ndi zizindikiro zomwezo zimene zikutsatira tsopano.

238 Ndipo ngati Lawi la Moto lija, kapena Kuwala, kumene ife tiri nako, sikunabereke Mzimu womwewo ndi umboni womwewo umene Iko kunabereka pamene Iko kunali mwa Yesu Khristu, ndiye ilo likanakhala lawi la moto lolakwika, mzimu wolakwika, chikanakhala chinthu cholakwika. Koma ngati Ilo likubala ndi kuchita ndendende basi zomwe Yesu ankachita, pamene Iye anati a. . . “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita.” Kulondola.

239 “Zochuluka kuposa izi iye adzazichita, chifukwa Ine ndikupita kwa Atate Anga.” King James ali ndi “zazikulu kwambiri,” koma tayang’anani mu lapachiyambi, limati “zochuluka.” Inu simungachite zazikulu kwambiri zirizonse. Iye anawukitsa akufa, ndipo anaimitsa chirengedwe, ndi chirichonse. Koma Iye akanakhoza kudzachita zochuluka za izo, chifukwa Mzimu Woyera sunali mwa Munthu mmodzi yekha, Khristu, Mwana wa Mulungu, Iwo unali mu Mpingo wadziko lonse. “Zochuluka kuposa izi inu mudzazichita, chifukwa Ine ndikupita kwa Atate Anga.” Oh, mai!

240 Utumiki Wake womwewo ukuyimiridwa kuno mmasiku otsiriza. Kodi Iye anali ndi utumiki wa mtundu wanji? Tayang’anani pa Iye, monga ine ndakhala ndikukubweretserani inu pansi, kutsimikizira kwa izo.

241 Tiyeni titenge Myuda mmodzi. "Iye anabwera kwa Ake omwe; Ake omwe sanamulandire Iye." Amuna oyamba omwewo amene anabwera kwa Iye anali Andreya ndi Filipo. Ine sindikudziwa zimene zinkachitika mu zokambirana zimenezo, mnyumbamo ndi Yesu usiku umenewo pamene iwo anamutsatira Iye. Koma tsiku lotsatira, Andreya anali wokhutitsidwa kwathunthu kuti ameneyo anali Mesiya. Iye anamuwonetsera iye chinachake, mpaka iye anapita molunjika kumene kwa Petro, m'bale wake, kapena—kapena Simoni, ndipo iye anati, "Usabwere tsopano ndipo tiye tizipita ndi kukawona ngati uyu ali." Iye anati, "Ife tamupeza Mesiya."

242 Ine ndikukhoza kulingalira Petro akunena tsopano, "Tsopano, Andreya, tsopano ndirole ine ndikuuze iwe chinachake, mwana. Tsopano, iwe ukudziwa kuti bambo athu okalamba aja anali Mfarisi wabwino. Ndipo iye anatiwuza ife, ine ndikukumbukira nditakhala pambali ya ngalawa tsiku lina, iwo anati kwa ine, iwo anati, 'Tsopano, tsopano, tsopano, Simoni, adadi akhala akuyembekezera kuti amuwone Mesiya. Ndipo mosakayika koma kuti Mesiya asanafike padzakhala mitundu yonse ya zinthu zikuchitika, mitundu yonse ya zochitika zidzawuka. Koma ndirole ine ndikhale wotsimikiza. . . ' Ndipo apo panali. Oh, inde. Anthu anabwera, anatsogolera masauzande, ndipo anawonongeka, ndi chirichonse. Koma, iye anati, 'Koma ndirole ine ndikuwuze iwe. Ife tikuyenera kukhala ndi Mawu, Simoni. Tsopano, Baibulo limati, Mose, wantchito wathu, wantchito wa Mulungu kwa ife, anatiwuza ife, kuti, "Ambuye Mulungu wathu akanati adzamuwukitse Mesiya uyu, ndipo Iye akanadzakhala mneneri wonga Mose." Tsopano, tsopano, Simoni, ngati iwe uti udzamuwone Iye mu tsiku lako. . . Ndine wokalamba kwambiri tsopano. Ine sindidzamuwona Iye mu tsiku langa. Koma ngati—ngati iwe uti udzamuwone Iye mu tsiku lako, kumbukira, Iye adzakhala Mulungu-Mneneri.'" Kotero Simoni anali ndi izo mu mtima mwake. Iye anati, "Chabwino, Andreya. Ine ndipita ku msonkhanoko."

243 Basi mwamsanga pamene iye anayenda mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu, Iye anati, "Dzina lako ndi Simoni. Abambo ako anali Yona." Izo zinakhazikitsa izo. Iye anapatsidwa makiyi aku Ufumu. Chimenecho chinali chizindikiro cha Mesiya.

244 Apa panabwera Myuda wina wokhazikika, anati, "Tsopano, dikirani miniti. Ngati Mesiya akanati abwere, Iye akanati adzabwere pansi kudzera mmakonde a Kumwamba, ndi kudzabwera ku kachisi wathu wamkulu, wabwino kwambiri amene ife tamumanga kuno kwinakwake," monga anthu ena kuzungulira kuno amakhulupirira kuti Iye adzabwera ku kachisi winawake. "Ndipo Iye adzabwera kumusi kuno, ndipo Iye adzawalira pansi *pano*, ndipo Angelo adzakhala akukupiza mapiko awo, chirichonse. Iwo amati, *Uyu* ndi Mesiya. *Uyu* ndi

Mesiya. *Uyu* ndi Mesiya.' Izo zidzakhala chomwecho."

245 Ine ndikukhoza kumumva Filipo akuti, "Dikira miniti. Iwe siuli Mwamalemba ndi izo. Ukhale ndi Mawu. Kodi Mose anatiwuza ife kuti Mesiya akanadzakhala chiyani? 'Ambuye Mulungu wanu adzadzutsa mneneri.' Iwe ukumukumbukira bambo wachikulire uja amene ankakonda kukhala kumeneko, wotchedwa Petro, Simoni?"

246 "Inde. Oh, munthu wokalamba ameneyo analibe maphunziro aliwonse? Inde. Ine ndikumukumbukira iye. Eya. Ine ndikumukumbukira iye."

247 "Iwe—iwe unagula nsomba zina kwa iye, ndipo amalephera kulemba lisiti lako."

"Eya. Chabwino, ine ndikumukumbukira iye. Ine ndikumukumbukira iye. Eya."

"Bwanji, pamene iye anayenda . . . Iwe ukuwadziwa abambo ake?"

248 "Chabwino, zedidi. Ndithudi ine ndinkawadziwa abambo ake mwabwino kwenikweni. Iwo anali Mfarisi weniweni, inde, wophunzira weniweni. Inde."

249 "Chabwino, pamene Simoni anayenda pamaso pa Iye, Iye anamuwuza iye limene dzina lake linali, ndi limene dzina la abambo ake linali."

250 "Ah, tsopano ine ndikukhulupirira kuti iwe wasokonekera. Ndirole ine ndipite, waona. Iye sadzawerenga konse malingaliro anga. Ine ndipita ndikafufuze."

251 Anayenda kupita kumeneko, mu Kukhalapo kwa Yesu, ndipo Yesu anati, "Taonani m'Israeli amene mwa iye mulibemo chinyengo."

Iye anati, "Kodi iwe unamuwuza Iye kuti umanditsatira ine?"

Anati, "Ayi."

252 Iye anati, "Rabbi," zimene zimatanthauza *mbuye* kapena *mphunzitsi*. "Kodi ndi liti Inu munandiwonapo ine? Ine ndangobwera mu msonkhano uno usikuuno. Ndi liti Inu munayamba mwandiwonapo ine?"

253 Anati, "Filipo asanakuyitane iwe, pamene iwe unali pansi pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe." Maso akewo!

254 Iye anati, "Rabbi, Inu ndi Mwana wa Mulungu. Ndinu Mfumu ya Israeli."

255 Koma apo panayima abale aakulu achipembedzo amenewo atayima pamenepo. Iwo anati, "Iwe ukudziwa chiyani? Iye amachita zimenezo ndi Belezebule." Mukuona? Iwo ankayenera kuti akayankhire kwa gulu lawo. Iwo anali ndi zowayenereza za padziko lapansi.

256 Iye anali ndi Zakumwamba, mwaona, chifukwa Mose anati, "Iye adzakhala mneneri," ndipo apa Iye anali, akutsimikizira kuti Iye anali Mneneri. Uko nkulondola. Iye anatsimikiziridwa. Kutumidwa Kwake kunatsimikiziridwa.

257 Chotero iye anati, "Tsopano, ine ndikudziwa kuti Munthu uyu amachita zimenezo. Koma Iye. . . " Iye ankayenera kuti akawayankhe osonkhana awo. Anati, "Ndi Belezebule Iye amachita izi, Iye amatulutsa ziwanda."

258 Yesu anapotoloka pamenepo, akuzindikira malingaliro awo. Iye anati, "Inu mukanena zimenezo monditsutsa Ine, Mwana wa munthu, Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha zimenezo."

259 Tsopano, iwo sananene konse izo momveka. Baibulo linati, "Iwo ankaganiza izo mmitima mwawo, ndipo Iye anazindikira malingaliro awo." Musunge zimenezo molondola. Inde, bwana. Anati, "Iwo, anazindikira mmitima yawo." Mukuona? "Iye—Iye—Iye anazindikira mitima yawo, zoganiza zawo."

260 Anati, "Tsopano, ngati inu mukunena zimenezo monditsutsa Ine, Mwana wa munthu, Ine ndikukhululukirani inu. Koma tsiku lina, kutali uko mdziko la Amitundu, mwaona, Mzimu Woyera udzabwera Ine nditatha kupita, ndipo Iye adzachita chinthu chomwecho. Ndipo kudzayankhula liwu limodzi motsutsa Iwo sizidzakhululukidwa konse, mdziko lino ngakhalenso mdziko liri nkudza."

261 Iye asanachoke pa dziko lapansi, Iye ananena zimenezi. Iye anati, "Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu." Ine ndikufuna kuti ndipange ndemanga iyi, ndipo nkutseka. "Monga zinali mmasiku a Loti, kumusi uko mu Sodomu," tiyeni tiwone chimene icho chinali.

262 Iye analozera, poyamba, ku—ku masiku a Nowa. Iye ananena zomwe iwo ankachita. "Kudya, kumwa, kukwatira, kuperekedwa mu ukwati."

263 Koma pamene Iye anabwera ku Sodomu, taonani chimene Iye anachita ku Sodomu. Ku Sodomu: Iye analozera kwa *izo* kwa m'badwo *uno*. Tsopano, kumbukirani, Achisodomu anali Amitundu. Mukuona? Zindikirani. Ndipo uko kunabwera Amuna atatu, tsiku lina, kwa Abrahamu.

264 Nthawizonse pamakhala mitundu itatu ya anthu, ndiwo: osakhulupirira, odzipangitsa-kukhulupirira, ndi okhulupirira. Ife tikadali nawobe iwo lero. Uko nkulondola. Osakhulupirira, odzipangitsa-kukhulupirira, ndi okhulupirira; Anthu a ku Sodomu, Aloti, ndi a Abrahamu.

265 Abrahamu anali ndi lonjezo. Iye anali wa gulu losankhidwa, loyitanidwa-kutuluka amene anali atadzilekanitsa yekha, monga Mpingo weniweni wa Mulungu wamoyo wadzipatula Wokha kuchoka ku zinthu za mdziko, chifukwa iye ankadalira

pa lonjezo la Mulungu. Kodi Angelowo anabwera kuti, poyamba? Kwa Abrahamu.

266 Chinachitika ndi chiyani? Awiri a iwo anapita kumusi mu Sodomu, Billy Graham wamakono, uko ku Sodomu, anakalalikira Uthenga, osati zozizwitsa zambiri, anakangowakantha iwo khungu. Kulalikira Mawu kumawakantha iwo ndi khungu. Kotero iwo sanakachite zozizwitsa zambiri, koma iwo ankayitana, "Tulukani mmenemo."

267 Koma panali Mmodzi amene anayankhula ndi Abrahamu. Inu mukudziwa, Abrahamu anali ndi kumverera kwachirendo. Inu mukudziwa, panali chinachake chokhudza Munthu ameneyo, chimene chinali chosinthika pang'ono, ndipo kotero iye anamuyang'ana Iye pang'ono pokha, inu mukudziwa. Ndipo iye anamuwuza Sarah, anati, "Tsopano, iwe ubwerere mu hema."

268 Chifukwa, tsopano mmasiku amenewo pamene mlendo abwera, akazi sankachita monga iwo amachitira lero. Iwo amachita kuthamangira panja ndi kukadzitulutsa okha panja, ndi kukatenga malo a mwamuna. "Ndipo iwe sungagulitse zimenezo, Yohane, pokhapokha ine nditakuwuza iwe kuti utero." Mukuona?

269 Akazi anali ndi khalidwe lochuluka mu tsiku limenelo. Iwo ankakhala mnyumba, inu mwaona. Chotero Iwo anapita kumeneko, ndipo Sarah anakhala mu hema.

270 Kotero iye anathamangira mkati, anati, "Sarah, ukande ufa pang'ono mwamsanga ndithu. Uchotse mibulu yonse mmenemo. Upange wina pamoto, mkate wina."

271 Anapita ndipo anakatenga mwana wa ng'ombe, ndipo anamupha iye. Ndipo anapita, anati, anawauza iwo, "Mumusende iye tsopano ndipo mumukonzekeretse iye."

272 Iye anapita kunja uko ndipo anakatenga chitsamba chakale cha ntchentche, ndipo anayamba kuthamangitsa ntchentchezo. Ndipo anatsuka mapazi Awo.

273 Iye ankadziwa, panali chinachake chaching'ono chimayaka mu mtima mwake. Iwe ukhoza kungodziwa izo, inu mukudziwa, zina. Iye anati, "Apo pali kutumidwako, ine ndikukhulupirira. Tsopano, chinthu chokhacho, ngati ine ndingathe kungowona kutumidwako kukutsimikiziridwa. Ine ndikhulupirira Iwo ali nako iko."

274 Iye anati, "Inu mukudziwa, Inu—Inu mwadutsa apa, kuti mudzandiwone ine. Ndi chifukwa chake Inu mwabwera njira iyi." Uko kunali kulondola. Mukuona? "Anakhala pansi pa mthundu, pang'ono pokha, ndipo anapuma." Kotero iye anatsuka mapazi Awo, pamene iwo ankakonzekeretsa zinthuzo.

Iwo anakhala pansi ndi kudya.

275 Ndipo—ndipo ameneyo anali Mulungu, Mulungu Wamphamvuzonse. Baibulo linati iye anali. Tayang'anani pamenepo ndipo muwone ngati ilo silinena ndi chilemba chachikulu A-m-b-u-y-e, Elohim. Uko nkulondola.

276 Monga winawake ankanenera, nthawi zambiri, ankati, "Inu simukukhulupirira kuti ameneyo anali Mulungu."

Ine ndinati, "Uyo anali Mulungu. Baibulo linati iye anali."

"Inu. . . " Anati, "Mulungu mu thupi limenelo, akudya nyama?"

277 "Izo ndithudi zinali. Baibulo linanena chomwecho. Inu simu—inu simuzindikira momwe Iye aliri wamkulu." Uko nkulondola. Ndine wokondwa kuti Iye akhoza kuchita zimenezo.

278 Chabwino, chinthu chokhacho, inu mukudziwa, ife tinangopangidwa ndi zipangizo sikisitini: petroliyamu, kuwala kwa dziko, kashiamu, potashi, ndi zinthu zochepa monga choncho. Chabwino, Iye anangofikira ndipo anatenga zodzaza mdzanja za izo, anapita "Psyii! Lowa mmenemo, Gabrieli," mwaona, Mngeloyo. Anatenga zodzaza mdzanja zina, anapita, "Psyii!" Anati, "Lowa mmenemo, Mikaeli." Anapita, "Psyii!" analowa mmenemo, Iyemwini. Ndine wokondwa kwambiri ndi zimenezo. Mukuona? Anabwera akuyenda, anati, "Ine ndikupita uko." Ameneyo ndiye Mulungu wathu.

279 Ena a masiku awa, zipangizo zonsezi zidzapita. Koma Iye adzanena kuti, "William Branham?"

Ine ndidzati, "Ine ndiri pano, Ambuye." Iye ndi wamkulu. Eya.

280 Anati, "Ine ndikuyenera kukadziyimirira Ndekha pamaso pa wantchito Wanga kumusi uko, ndipo ine ndikufuna kuti ndikakhale munthu monga iye." Kotero Iye anangoyenda, anakakhala pansi pamenepo, fumbi liri pa zovala Zake, anakakhala pansi ndipo anadya. Anakakhala pansi.

281 Iye anapitirira kumayang'ana chaku Sodomu, inu mukudziwa. Abrahamu anadziwa kuti panali chinachake, chifukwa amenewo ndi malo awuthakati akale, inu mukudziwa. Kotero iye anapitirira kumaganizira za zimenezo, monga choncho. Iye anati . . .

282 Tsopano, kumbukirani, dzina lake linali Abram, ndipo dzina la Sarah linali S-a-r-r-a, Sarra. Ndipo masiku angapo izo zisanachitike, Mulungu anali atakumana naye iye mmasomphenya ndipo anasintha dzina lake kukhala Abraham, ndipo dzina la mkaziyo kukhala Sarah, S-a-r-a-h. *Sarah*, "mfumukazi." *Abraham*, "atate wa mafuko."

Chotero Iye anati, "Abraham."

283 Abraham anati, "Oh—oh. Ine ndikudziwa kuti ndimalondola. Pali chinachake chokhudza Munthu ameneyo chimene chiri chosiyana."

284 "Abraham, alikuti mkazi wako," S-a-r-a-h, "Sarah? Alikuti mkazi wako, Sarah?"

Iye anadziwa pomwepo. "Oh," iye anati, "iye ali mu hema."

Ndipo Baibulo linati, "Iyo inali kumbuyo kwa Iye. Hemayo, kumbuyo kwa Iye."

285 Iye anati, "Abraham, Ine. . ." Mlowammalo waumwini; Mmodzi yemweyo amene anayankhula ndi iye. "Ine ndidzakuchezerani inu molingana ndi nthawi ya moyo, mwaona, ndi Sarah, ndipo inu mudzakhala ndi mwana uyu amene mwakhala mukumuyembekezera. Ndiwe wa usinkhu wa zaka handiredi tsopano, ndipo mkaziyo ali ndi nainte. Koma, Ine—Ine ndidzakupatsa iwe mwana uyu amene Ine ndinakulonjeza iwe, chifukwa iwe wakhala wokhulupirika, pomuyembekezera."

286 Ndipo Sarah, kumbuyo mu hema, iye anati, "Huh." Iye sananene izo mofuula. Iye anaseka, mwa iyemwini, anati, "Ine, mkazi wokalamba, kukhalanso ndi zosangalatsa kachiwiri, ndipo mbuye wanga, wokalamba monga choncho?" Anati, "Izo sizingatheke basi. Munthu ameneyo, kodi Iye akuyankhula chiyani?"

Mngeloyo anati, "Nchifukwa chiyani Sarah anaseka?" Hum!

287 Chinali chiyani chimenecho? Iye anawuyamba waku Sodomu. Mwamsanga kutatha kuchezera kwa Mngelo ameneyo, chizindikiro chotsiriza icho chimene chinaperekedwa, chizindikiro chotsiriza chimene chinaperekedwa, Sodomu anawotchedwa.

288 Yesu anati, "Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu."

289 Mulungu wakhala akuchita ndi Mpingo Wake, nthawi yonseyi, kupyolera mu zizindikiro, zodabwitsa. Koma chinthu chotsiriza chinali chakuti Mulungu awonetseredwe mu thupi la Mpingo Wake, monga Iye anali mu mnofu wa munthu pamenepo, ndi kuwonetsera chizindikiro chomwecho, chimene Mesiya anali atadziyimirira kale Iyemwini pakati pa anthu, basi moto usanagwe pa tsiku lotsiriza: choyenereza, kuti atsimikizire kuti Mawu amene Yesu analonjeza ndi Choonadi. Tiyeni tipemphere.

290 Atate athu Akumwamba, iwo ndi Mawu Anu, kutsimikizira kwa kutuma. Amenewo ndi Mawu Anu, Atate. Ife tikhoza kungowayankhula Iwo. Ine ndikupemphera kuti Inu muwatsimikizire Iwo, Ambuye. Ndipo ine ndikudziwa kuti. . . Ine ndi-. . .ndikupemphera kuti Inu mundikhululukire ine chifukwa cha manjenje anga, ndipo wanga—ndi umbuli wanga, zonse za izo, ndi kuzichotsa izo mmalingaliro a anthu, njira yanga yosauka, yodukaduka yoyesera kuti ndibweretsere uthenga. Ndipo—ndipo Mzimu Woyera ukumenya pa ine, ine—

ine—ine sindikudziwa momwe ndingachitire koma kungopereka njira kwa Iwo, Atate, ndakhala pano ndi amuna ndi akazi amene ali amwendamnjira ndi alendo.

291 Pamene, dziko lonse likugwedezeka, lero. Iwo—iwo akuti tsopano, mmasiku pang'ono, tsopano iwo amuzungulitsa munthu kuzungulira dziko, mu kanjira, amutengera iye kuzungulira dziko, kuyesetsa kuti amutengere munthu mmwamba ku mwezi. Dziko lonse, likunjenjemera ndipo likugwedezeka. Mafuko aang'ono, kulikonse, ali ndi mizinga yomwe iti iphulitse dzenje mu nthaka, mapazi handiredi ndi fifite kuya kwake, kwa mamailosi thuu-handirede-ndi-fifite kapena firii-handirede mbali zonse zonse. Atatu a iyo pa nthawi imodzi akhoza kumiza dziko lonse lapansi. Dziko lonse liri mu chikhalidwe chamanjenje.

292 Mipingo yapita kutali ndi Mawu. Pali mitundu yonse ya mabungwe ndi zipembedzo zimene ziri ndi zoyenereza za padziko lapansi. Ndipo—ndipo ngati iwe siuli wa iwo, iwe sungalowetse mutu wako mu umodzi wa mipingo yawo.

293 Koma, komabe, monga izo zinali kumbuyo uko mu nthawi ya Nowa, monga izo zinali kudutsa mu Baibulo, Inu mudzatumizabe aneneri Anu ndi antchito, Ambuye, ali ndi kutumidwa, ndi chitsimikiziro kumbuyo kwake. Mulungu, ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha zimenezo, kuti Inu munalonjeza izo.

294 Ndipo tsopano, Ambuye, Inu munati, "Musawope ayi, Nkhosa zapang'ono. Nkhosa Zapang'ono, ndi chifuniro chabwino cha Atate anu kuti akupatseni inu Ufumu."

295 Inu munati, "Monga izo zinali mmasiku a Nowa, pamene gulu laling'onolo linangopulumutsidwa ndi madzi, chomwechonso izo zidzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu." Masiku a Loti, pamene. . . Mu nthawi ya Nowa, "Iwo ankadya, kumwa, kukwatira, kuperekedwa mu ukwati." Ndipo tayang'anani pa izo lero, Atate, ife tikuziwona izo. Tsopano, izo zinali kwa dziko lochimwa limene linkachita zimenezo.

296 Ndipo tsopano tayang'anani pa masiku a Loti, momwe kupotoza, amuna ogonana okhaokha! Oh, momwe dziko, dziko lonse, ochuluka a boma lathu amezedwa ndi zimenezo, ndipo konsekonse. Oh, ndife odyedwa ndi mphutsi, Ambuye, ndi adierekezi ndi mphamvu ya mdani.

297 Dziko lonse likuchita mantha mpaka ku imfa. Ndipo lathu lonse. . . Ngakhale fuko lathu liri ngati mnyamata wamng'ono akudutsa pa manda usiku, akuyimba muluzi, kuti asachite mantha. Ife tikudziwa kuti izo ziri pakhomo.

298 Mpingo, Ambuye, Inu munati, "Kwezani mmwamba mawondo anu. . . Mudzakweze mmwamba maso anu pamene zinthu izi zidzayamba kuchitika. Chiwombolo chanu chikuyandikira pafupi."

299 Mzimu Woyera watsanuliridwa pa Mpingo Wanu. Inu mwawayitana anthu a fuko lirilonse, achi Mexico, azungu, Anglo-Saxon, achikuda, achi Ethiopia, mitundu yonse yosiyanasiyana, konse kudutsa mdzikoli. Monga amishonare Anu aang'ono akale a Mzimu Woyera anapita, anjala, ovutika, ambiri a iwo anaphedwa, anapachikidwa, kusekedwa, ndi china chirichonse. Iwo ankapita opanda mpingo waukulu uliwonse kuti uwathandizire iwo. Iwo ankapita pa kutuma kwa Mulungu, ndi, "Zizindikiro izi zikuwatsatira iwo amene akhulupirira." Ine ndakomana nawo iwo ku ntchito ya umishoni kutaliko, Ambuye. Ife takhala tiri ndi mphamvu yayikulu ya Mulungu, kuti tiziyankhula ndi malirime, kutanthauzira malirime. Ife takhala tiri ndi maubatizo a Mzimu Woyera, ziwonetsero za mphamvu.

300 Ndipo tsopano, Ambuye, monga Inu munamutengera Abrahamu, kuimirira Osankhidwa, oyitanidwa-atuluke. Inu munamubweretsa Abrahamu kudutsa mchipululu chimenecho, wolekanitsidwa. Inu munamuwonetsa iye mitundu yonse ya zizindikiro. Koma chizindikiro chotsiriza chinali pamene Mulungu, Mwiniwake, anadziwonetsera Yekha mu thupi.

301 Yesu, Inu munati, "Monga izo zinali mu tsiku limenelo, chomwechonso izo zidzakhala pamene Mwana wa munthu adzabwera." Bwerani, Ambuye. Awa ndi Mawu Anu, molunjika momwe ine ndikuwadziwira Iwo. Ine ndikuwakhulupirira Iwo, Ambuye. Alipo ena pano amene akuwakhulupirira Iwo. Mulole izo zichitikenso, Ambuye. Mulole izo zichitike mu Tempe, ngati chitsimikiziro cha kuyandikira kwa pafupi kwa Ambuye Yesu. Perekani izi, Ambuye. Izo zingatilimbikitse tonsefe, Ambuye. Izo zingawalimbikitse abale awa. Izo zingawalimbikitse atumiki Anu konsekonse. Izo zingawalimbikitse anthu osonkhana. Izo zingatipangitse ife tonse kukondwa. Perekani izi, Atate.

302 Tsopano, motalika momwe ine ndingathe kupitira ndi kuyankhula Mawu Anu. Tsopano, Ambuye, izo zikuyenera kutengera Inu kuti mupange kutsimikizira kumeneko. Ine sindingathe. Koma ngati uku ndi kutumidwa, ine ndalalikira Choonadi, ine ndikukhulupirira, Atate Akumwamba, kuti Inu mudzatsimikizira Iwo ndi zizindikiro zimene Inu munalonjeza kuti zikanadzakhala mu tsiku lino. Perekani izi, tsopano. Ine ndikudzipereka ndekha kwa Inu, ndi mpingo uno, ndi Mawu. Tsopano, Atate, ife tiyembekezera pa Inu, ngati Inu muti mungotiwonetsera ife kuti Inu muli pakati pathu. "Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita." Ndilo lonjezo Lanu.

303 Ndipo, Atate, momwe izo ziti ziwalimbikitsire ena a abale anga pano, momwe izo ziti ziwulimbikitsire mpingo; kuti chinachake chimene sichiri nthano chabe, chinachake chimene inu munanena, "Eya, ine ndamva izi zikulalikidwa nthawi zonse." Koma, Atate, mulole iwo awone kuti Ndinu

Mulungu amene mumasunga Mawu Anu. Tsopano, izo zitengera zochuluka kuposa ine, Atate. Izo zitengera mpingo uwu wonse mu mgwirizano umodzi. Izo zitengera chikhulupiriro chenicheni kuti chichite izo. Koma ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mupereke izo kwa ulemelero wa Mulungu, mu Dzina la Yesu. Ameni.

304 Tsopano, abwenzi, mzere wa pemphero. Oh, ine ndikupepesa. [M'bale O'Donnell akuti, "Pitirirani nazo. Izo zonse ziri bwino."—Mkonzi].

305 Mundikhulululukire ine chifukwa cha makhalidwe anga otengeka, oduladula pa guwa. Ine—ine ndikupempha kuti muchite zimenezo. Koma ine ndangomaliza kumene kuwerenga *Pre-Nicene Council*. Ndipo ndinatenga *Two Babylons* ya Hislop, ndi *Pilgrim Church* ya Broadbent, *Pre-Nicene Council*, *Nicene Council*, ndi *Post-Nicene Council*, *Nicene Fathers*, kuwona momwe Mzimu Woyera unkawasunthira iwo. Iwo analibe ngakhale guwa mu mpingo wawo. Iwo analibe kanthu ngati mtanda. Roma Katolika anapitirira ndi mwambo, ndi mtanda. Koma achi orthodox enieni anakhalabe mwabwino, anali ndi nyumba zazing'ono zopanda kanthu koma madwale chabe. Ndipo iwo ankakhoza. . . Munthu wina waumulungu ankakhoza kufotokoza Mawu a Mulungu, ndipo mphamvu ya Mulungu inkatha kugwa. Iwo ankangokweza manja awo ndi kumutamanda Mulungu. Iwo ankakhoza kuyankhula ndi malirime, ndipo zizindikiro ndi zodabwitsa zinkawatsatira iwo. Inde, bwana.

306 Polekapu, Ignatius, Martin, Ireniasi, Columba, oh, mai, Justin, ndi angati ena a aumulungu enieni amene sankalolerana ndi mpingo winawo nkomwe, mbali ya Chiroma ya izo. Iwo anakhalabe akatolika. Ife ndi akatolika, nafenso, chikatolika cha atumwi. Tsopano, *katolika* amatanthauza "wakonsekonse."

307 Koma Roma Katolika anatengeramo mtanda ndi mbalume, ndi zina zotero monga choncho, ndipo anati, "Osati Baibulo." Iwo, "Mulungu anali mu mpingo Wake."

308 Mulungu ali mu Mawu Ake. Baibulo linatero, "Ngati munthu aliyense ati adzachotse kapena kuwonjezera chirichonse kwa Iwo, yemweyo lidzachotsedwa, gawo lake, kuchoka mu Bukhu la Moyo." Ife timakhulupirira basi zomwe Mulungu ananena, ndipo ndizo zonse. Tsopano, kotero, ife timakhulupirirabe Uthenga umenewo.

309 Tsopano, pali anthu odwala pano usikuuno. Ine ndalalikira kwa inu, kuti Mulungu amatsimikizira kutuma Kwake. Uko nkulondola. Mulungu amayang'anira Mawu Ake, kuti awatsimikizire Iwo. Chinthu chokhacho chimene Iye akuyesetsa kuti achite ndi kuti apeze mtima umene Iye angathe kulowamo.

310 Tsopano, musaganize kuti muchita izo mopyoletsa muyezo. Inu simutero. Kodi inu mungalingalire a—nsomba yaying'ono

yotalika pafupifupi theka la inchi, uko pakati pa nyanja kutali uko, ikuti, "Ine ndikuyenera kumwa madzi awa mosamalitsa. Akhoza kundithera ine"? Ndithudi ayi. Chabwino, inu simungathe konse kumaliza mphamvu ya Mulungu ndi ubwino wa Mulungu. Inu ndithudi simungathe, kotero mungotsegula . . .

311 Inu mukuti, "Chabwino, ine ndinalandira Mzimu Woyera." Oh, apo pali basi—basi . . .

312 Miyamba yonse yadzaza ndi Iwo. Mukuona? Mulungu akungoyesera . . . monga . . . Ngati iyo yonse inali, miyamba yonse, ikanakhala payipi yayikulu kwambiri yoima, ndipo inu nkukhala ndi mng'alu umodzi wawung'ono. Iye akuyesera kuwunjika . . . Madzi amenewo angayesetse kudzikakamizira okha kuti atuluke. Umo ndi momwe Mzimu Woyera ukuyesetsera kudzikakamizira Wokha mwa inu, monga chomwecho, monga chomwecho, kuyesetsa kuti ukupangitseni inu kuti muwukhulupirire Iwo. Ine ndikudziwa kuti icho ndi Choonadi. Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti . . . Kodi iwo anapereka . . .

313 Kodi iye anapereka makadi a pemphero? Ine ndipemphera. Ine ndikukhulupirira kuti iye anatero. [Abale akuti, "Inde."—Mkonzi]. Chabwino. Kodi . . . Iye ali kuti? Chiyani? Mundikhululukire ine. Wani mpaka fifite. Chabwino. Ife sitingathe kuwayimitsa iwo onse pa kamodzi. Chotero tiyeni ife tiwayimitse mwina . . . Bwanji, izo ziri bwino, ingoyimani njii, mungosuntha, mwinamwake mzere waung'ono uwu apa usunthire mmbuyo, kuchitira kuti iwo akhoze kusuntha pang'ono. Pali galasi la madzi, ine ndikukhulupirira, liri pamenepo, ngati inu mungapenye. Chabwino.

314 Tiyeni tikhale ndi nambala wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni. Aloleni iwo ayime. Nambala wani, ndani ali nalo ilo? Khadi la pemphero nambala wani? Ilo ndi khadi la pemphero basi ndi nambala pa ilo. Nambala wani, thuu, firii, foro, monga choncho. Nambala wani, khadi la pemphero, ndani ali nalo ilo? Pali ndithudi chinachake cholakwika.

315 Yankhulani izo mu Spanishi. Kodi nambala *wani*, mu Spanish ndi chiyani? [Winawake akuti, "Uno."—Mkonzi]. Uno. Uno, ndani ali nalo?

316 Nambala wani? Mukuti chiyani? Chabwino, apa pomwe. Nambala thuu, ndani ali nalo ilo? Nambala firii, foro, faivi, sikisi, seveni, eyiti? Wani, thuu, firii, mungoyima *apa* pomwe. Ife tipanga mzere. Huh? Eya. Izo ziri bwino. Chabwino. Izo ziri bwino. Chabwino. Wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni. Aloleni iwo abwere. Bwerani muzungulire mbali *iyi*, ngati inu mungathe.

317 Ngati inu simungathe kuimirira tsopano, kwezani dzanja lanu. Ife tiwonetsetsa kuti inu mufike kuno. Ife tiwona. Winawake akunyamulani inu kukufikitsani kuno. Mukuona?

318 Sikisi, seveni, eyiti, naini, teni. Leveni, thwelovu, sartini, fortini, fifitini, sikisitini, seventini, eyitini, naintini, twente. Aloleni iwo abwere, kuyambira pa wani mpaka twente tsopano, dzifoletseni nokha *apa*. Chabwino. Uko nkulondola.

319 Tsopano, ngati inu muli ndi makadi anu, bwerani, abwenzi. Musati—musati—musakhale mmbuyo, chifukwa inu muzimubera munthu wina zimenezo, inu mwaona. Musachite mantha kuti mubwere, ngati inu munatenga khadi lanu. Bwerani, ngati iwo anakupatsani inu khadi.

320 Tsopano, mnyamatayo amabwera ndi makadi awa, poyamba. Iye amadzaima pamwamba apa ndipo amadzawasakaniza iwo, pamodzi, fifite kapena handiredi, kapena chirichonse chimene iye amachita. Amapita pansi pa mzere pomwe, nkumupatsa aliyense. Munthu mmodzi akhoza kutenga "wani," mmodzi winayo "teni," mmodzi winayo "fifite," ndipo winayo "nainte," monga choncho. Ife sitimadziwa kumene iwo ali. Iwo onse amamwazikana. Izo zimamuchoka mnyamatayo chotero iye samadziwa chiyani. Ndiye, mnyamatayo samadziwa pamene ine nditayambire kuyitana, usiku umenewo. Chifukwa, mwaona, ine sindimadziwa, inemwini. Ine ndikhoza kuyambira . . . Ndi angati amene anakhalapo mmisonkhano mmbuyomu, ndipo akudziwa kuti ndimangodumpha mozungulira izo? Izo zonse nzabwino. Mukuona?

321 Kotero, nthawi zambiri, anthu amawopa kubwera kutsogolo, chifukwa machimo awo amadzatchulidwa kuno. Tsopano, ngati inu mwachita chirichonse cholakwika, ndipo inu simukufuna kuti icho chitchulidwe, inu kulibwino mukhale kunja, ndizo zonse, chifukwa Iye ndithudi achita zimenezo. Uh-huh. Ndi angati akudziwa kuti izo ndi zoona? Inde, bwana. Ndithudi ndi zoona. Tsopano, ngati inu muli—ngati mukutsutsidwa ndipo muli pansi pa tchimo, bwanji, inu musabwere. Koma ngati inu simuli, ngati inu muli pansi pa Magazi, bwerani. Mukuona? Chabwino.

322 Tsopano, chabwino, chabwino, ife tingoyambira pomwe apa ndi kuwona kumene ife tingapite.

323 Tsopano, ndi angati muno akudwala, ndipo abwera ndipo sanapeze khadi la pemphero, mwachedwa kwambiri kapena chinachake? Kwezani mmwamba manja anu, paliponsepo, mchipinda muno, chabwino, mulibe khadi la pemphero.

324 Tsopano, panali mkazi wamng'ono amene anadutsa mu unyinji. Mwinamwake iye analibe khadi la pemphero, koma iye anakhudza mphonje ya chovala Chake. Izo zinachita zimenezo. Chabwino. Anakhudza mphonje ya chovala Chake, ndipo iye anapangidwa wamphumphu.

325 Tsopano, inu kunja uko amene mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, inu amene mukukhulupirira izi kwenikweni ndi mtima wanu wonse, inu mungoti, "Ambuye Yesu, ine

ndikukhulupirira izi ndi mtima wanga wonse, ndipo ine ndikuvomerezani Inu, ndipo ndikukhulupirira kuti . . . Ine ndikudziwa kuti M'bale Branham samandidziwa ine, kapena kudziwa chirichonse cha ine. Ndipo ngati Inu mutangondilola ine kuti ndikhudze chovala Chanu!" Tsopano, Baibulo limati . . .

326 Tsopano, atumiki achitira umboni za izi. Baibulo limanena, kuti, "Yesu Khristu ndi Wansembe Wamkulu, pakali pano, amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zofooka zathu." Kodi izo ndi zoona? "Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zofooka zathu." Iye ali, pakali pano.

327 Chabwino, ndiye, ngati Iye ali Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zofooka zathu, kodi Wamkulu Wansembeyo angachite motani pamene Iye wakhudzidwa? Ngati Iye ali Yesu yemweyo amene Iye anali kumbuyo uko, Iye angachite mwanjira yomweyo. Iye sangasinthe njira Zake. Iye sangatero.

328 Ngati Iye ananena kumbuyo uko, "Chabwino, Ine ndinawapulumutsa iwo chifukwa iwo anakhulupirira pa Ine, koma lero ine—ine—ine ndiwapulumutsa iwo chifukwa iwo ali ndi ndalama zambiri," Iye sangachite zimenezo.

329 Iye akuyenera kukhalabe ndi kachitidwe Kake koyamba. Mukuona? Pamene Mulungu apanga chigamulo, icho chimakhala changwiro. Icho sichingasinthidwe, nkomwe. Mulungu samasintha konse dongosolo Lake, mwaona, kotero ngati Iye ali Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zofooka zathu, ndipo inu nkumukhudza Iye ndi chikhulupiriro chanu . . .

330 Tsopano, Iye alibe manja aliwonse pa dziko lapansi koma anga ndi anu. Nkulondola uko? "Ine ndi Mpesa; inu ndinu nthambi." Tsopano, Mpesa sumabala chipatso, iwo umatero? Nthambi zimabala chipatso. Kotero Mpesa umangopereka mphamvu ku nthambi, koma, inu mukuona, nthambi . . . Mpesa sunapangidwe kuti uzitero, mwaona, Iye ali mu Ulemelero, Iye ndi Mzimu Woyera, tsopano, Iye samabala chipatsocho, koma Iye amapereka mphamvu kwa inu ndi ine, kuti ife tizikhoza kumvetsetsana wina ndi mzake, kupyolera mmaliwu, Iye amayankhula kupyolera mwa ife ndipo amachita ntchito Yake, kutsimikizira kutuma kumene ife tatumidwa kuti tichite. Inu mukumvetsa izo tsopano, aliyense? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

331 Tsopano inu mupemphere, ndipo munene kuti, "Ambuye Yesu, ine ndikhulupirira izi ndi—ndi mtima wanga wonse. Ine—ine—ine ndikhulupirira izo moona ndi zonse zimene ziri mwa ine. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Inu mutero—mundipanga ine kukhala wamphumphu. Ndipo ine ndi, ndi mtima wanga wonse, ndiyesetsa kukhudza mphonje ya chovala Chanu, ndikudalira

kuti Inu mundichiritsa ine,” tsopano, inu mungokhulupirira zimenezo, “kapena kwa wokondedwa.”

332 Tsopano, ine ndikufunsani inu. Ndi chimene... Tsopano, inu mukudziwa kuti ndine wa chipentekoste. Ine—ine ndimakhulupirira mu kufuula, kuwalemekeza Ambuye. Koma ine ndikupemphani inu kuti muchite ichi. Tsopano, pamene ife tikubwera, ine ndikufuna kuti inu mungokhala molemekeza momwe inu mungathere. Tsopano, mungodzibisa nokha kutali tsopano. Muyike kukayikira kwanu konse kutali, ndipo mungoti, “Tsopano, Ambuye, ndithandizeni Inu ine.” Mulungu achita izo, ngati inu mutangokhulupirira izo.

333 Tsopano, tsopano, apa payima mkazi. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye mmoyo mwanga.

334 Tsopano, aliyense amene ali pa *ichi* apa. Nthawizina ine sindimadziwa chimene ndikunena; ngati izo zikandikhudza ine, iwo amakhala masomphenya. Tsopano ngati inu... Kodi mukukhoza kundimva ine bwino bwino tsopano? Chabwino. Tsopano mungokhala molemekeza kwenikweni.

335 Tsopano, apa payima mkazi. Tsopano, apa pali chithunzi chokongola cha Baibulo. Ndife alendo kwa wina ndi mzake. Ine sindikukudziwani inu. Tsopano, inu mukhoza kundidziwa ine, podziwa kuti ndine M’bale Branham. Koma ine sindikukudziwani inu, mwanjira iliyonse.

336 Tsopano, ichi ndi chithunzi monga icho chinali mu Yohane Woyera 4. Yesu anakomana ndi mkazi amene Iye anali asanamuwonepo, kapena iye sanamudziwe konse Iye. Iye anadziwa kuti Iye anali Myuda, koma ndizo zonse zomwe iye ankazidziwa. Ndipo kenako Yesu anayankhula naye mkazi uyu kwa kanthawi pang’ono. Kodi Iye ankachita chiyani? Iye ankawukhudza mzimu wake. Mukuona?

337 Iye anali ndi kusowa kuti apite ku Samariya. Ndipo pamene Iye ankapita ku Samariya, Iye anakomana ndi mkazi uyu. Bwanji? Atate anamutsogolera Iye ku Samariya. “Upite uko ku Samariya.”

338 Iye sankadziwa choti achite. Mkazi uyu anatulukira. Iye anaganiza, “Mwinamwake ichi ndi chimene Atate akufuna.” Chifukwa, Iye anati...

339 Iye atatha kumuchiza munthuyo pa... amene anali wolumala, osati wolumala, koma ine ndikuganiza kuti iye akhoza kukhala kuti anali ndi matenda osakula. Mu Yohane Woyera 5, mutu wotsatira, ine ndikukhulupirira ndi umenewo. Iye anapita pa dziwe la Betisaida, ndipo apo panagona munthu yemwe anali wolumala kwa zaka zingapo, anali ndi zofooka. Tsopano, iye ankakhoza kuyenda. Koma Mngelo ankatsika pansi ndipo ankavundula dziwelo. Inu abale mukudziwa pamene ndikuyankhula. Ndipo kenako Yesu anadzabwera pamenepo, ndipo anati, iye anati, za kupita ku dziwelo, iye

anati, "Ine ndiribe aliyense woti andithandize ine. Winawake akhoza kuchita bwinoko kuposa ine. Iye akhoza kundikankhira ine ku dziwelo," mwa kuyankhula kwina.

340 Iye anati, "Nyamula mphasa yako ndipo ulowe m'nyumba mwako." Iye ananyamula mphasa yake ndipo anawuyambapo.

341 Tsopano, Yesu sanachiritse winanso wa iwo, ndipo apo panali unyinji, masauzande. Nchifukwa chiyani Iye sanachite zimenezo? Apo pali mmodzi wa osonkhana, wa ife atumiki. Mulungu wodzaza ndi chifundo. Nkulondola uko? Unyinji wa olumala, akhungu, osayenda, opinimbira, mitundu yonse ya anthu. Kodi Baibulo linanena zimenezo, abale? Ndipo Iye anapita kwa munthu mmodzi amene anali ndi zofooka. Iye sanali wakhungu. Iye amatha kuyenda. Iye mwinamwake anali ndi vuto la thumbo. Iye mwinamwake anali ndi TB yokhalitsa. Izo sizikanati zimuphe iye. Iye anali nazo izo kwa zaka twente eyiti, ndipo izo sizinali zoti zimupha iye. Ndipo Iye anapita kwa munthu ameneyo. Bwanji? Kenako, anangomuchiritsa ameneyo, ndipo anachokapo.

342 Bwanji ngati Iye akanati abwere ku Tempe usikuuno ndi kudzachita zimenezo? Iwo akanamutsutsa Iye apo pomwe. Nkulondola uko, abale? Iwo akanamutsutsa Iye. Koma, kumbukirani, Yesu anamudziwa munthuyo ndipo anadziwa kuti iye anakhala ali mu chikhalidwe chimenecho nthawi yonseyi. Kodi icho ndi chimene Iye ananena?

343 Tsopano, pamene Ayuda anamupeza munthu uyu, iye anawauza iwo Amene anachita izo. Iwo anamupeza Yesu ndipo iwo anamufunsa Iye. Inu mukuganiza kuti iwo akanamufunsa Iye usikuuno? Zedi.

344 Kodi Iye ananena chiyani? "Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha, koma chimene Iye awawona Atate akuchita: chimenecho amachita Mwana chimodzimodzi." Nkulondola uko? Ndiye, molingana ndi Mawu Ake omwe, Iye samachita kanthu mpaka Mulungu atamuwonetsera Iye mmasomphenya choti achite.

345 Kumbukirani Eliya, mu ulaliki wathu usikuuno? "Ine ndachita zonsezi mwa kulamulira Kwanu." Mneneri aliyense wa Ambuye amangopita momwe Ambuye akumutsogolera iye.

346 Tsopano tiyeni tifanizitse izo. Tsopano, Khristu ndi Mzimu Woyera umene uli muno tsopano. Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti ine ndinamverera kutsogozedwa kuti ndibwere ku Arizona. Yesu anamverera kutsogozedwa, ankayenera kuti apite ku Samariya. Ine ndinamverera kutsogozedwa kuti ndidzakhale ndi msonkhano wa machiritso ku Tempe usikuuno, sindinakhalepo nawo umodzi kumtunda kuno. Ine sindikudziwa chifukwa chake.

347 Chabwino, zachitika kuti ndinu munthu woyambirira kuntunda kuno. Ndi zimenezotu pamenepo, Yohane Woyera

4, ndendende kachiwiri. Ine sindikukudziwani inu. Inu simukundidziwa ine. Ine sindikudziwa chinthu chimodzi. Inu mukhoza kukhala wochimwa. Inu mukhoza kukhala wachinyengo. Inu mukhoza kukhala mu chigololo. Inu mukhoza kukhala woyera waumulungu. Inu mukhoza kukhala mukudwala. Inu mukhoza kukhala mukumuimira winawake. Inu mukhoza kukhala ndi mavuto azachuma. Ine sindikudziwa chimene inu muli nacho. Ine sindikudziwa kanthu za inu. Tsopano, uko nkulondola, ine sindikudziwa. Tsopano, ngati ndine mlendo, kuti wosakhulupirira wina akhoza kukhala ali pafupi, kwezani dzanja lanu, ngati ife tiri, ngati izo—izo nzoona. Mukuona? Tsopano, ngati Mzimu Woyera. . . pokhudza mzimu wake.

348 Tsopano, ife tonse tayima pano, mwamuna ndi mkazi, chimodzimodzi monga iwo anachitira. Ndipo Yesu anayankhula kwa iye mpaka Iye anapeza chimene chinali cholakwika ndi iye. Nkulondola uko? Tsopano, onse amene akudziwa kuti izo nzoona, anene, "Ameni." [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Iye anapeza chimene vuto lake linali, ndipo Iye anamuuza iye limene vuto lake linali.

349 Ndipo iye anati, "Bwana, Inu mukuyenera kukhala mneneri." Mwaona, iwo anali asanakhale ndi aneneri kwa pafupifupi zaka foro handirede. Iye anati, "Inu mukuyenera kukhala mneneri. Tsopano, ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera, ichi chidzakhala chizindikiro cha Mesiya. Iye adzatiwuza ife zinthu zonse." Nkulondola uko?

Chabwino, Yesu anati, "Ine ndine Iye amene akuyankhulayo."

350 Tsopano, ngati chimenecho chinali chizindikiro cha Mesiya pamenepo, ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; kokha, m'mawonekedwe a Mzimu Woyera, pogwiritsa ntchito thupi langa, mzimu wanga pamene ine ndikuwupereka kwa Iye, ndipo nkundiwuza ine pamene vuto lanu liri, inu mukhoza kudziwa ngati izo zinali zolondola kapena ayi, chifukwa ndinu mboni ya izo. Tsopano, ngati inu. . .

351 Ngati ine ndikanakhala ndi msonkhano wamachiritso, ine nkubwera apo, nkudzati, "Ulemelero kwa Mulungu! Mukudwala, mlongo?"

"Inde. Ine ndiri ndi TB"

352 "Ulemelero kwa Mulungu!" Nkudzayika manja pa inu. "Aleluya! Landirani machiritso anu."

353 Tsopano, abale abwino ambiri, monga M'bale Oral Roberts ndi iwo, iwo ndi amuna enieni a Mulungu. Imeneyo ndi mphatso yawo. Iwo amati, "Ulemelero kwa Mulungu! Ine ndikukhulupirira zimenezo. Inu?"

"Inde."

354 Ine ndikukhulupirira kuti inu mukhala bwino. Ndithudi, ine ndikukhulupirira zimenezo. Inde, bwana. Ine ndikukhulupirira. Inu mungapite kwa abusa anu, ngati muli Mkhristu, kapena chirichonse monga choncho, ine ndikukhulupirira inu mungatero—inu mungachite zimenezo.

355 Koma tsopano bwanji ngati Iye atabwera ndi kudzakuuzani inu chinachake chimene inu mwachita. Tsopano, inu mukhoza kudziwa ngati icho chiri choona kapena ayi. Ndipo ngati Iye angakuuzeni inu chimene chachitika, ndithudi inu mukhoza kukhulupirira ngati Iye angakuuzeni inu zimene ziti zidzachitike. Ndi zoona zimenezo? [Mlongoyo akuti, "Zoona."—Mkonzi].

356 Tsopano, ndi angati akukhulupirira kuti izo zingakhale umboni, ngati Iye atachita zimenezo, kuti Iye ndi Yesu Khristu Mesiya, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Tsopano, kumbukirani, osati ine. Ayi. Ine ndiri ngati maikrofoni iyi, yosayankhula mwangwiro. Ine ndingadziwe bwanji? Ine ndavomereza kwa inu, ndi kwa iye, ndi tonse kwa wina ndi mzake, ife sitiri, ife sitinayambe tawonanapo wina ndi mzake. Kotero izo zitengera mphamvu yochokera kwinakwake.

357 Tsopano, inu mukhoza kukhulupirira monga ena a iwo anachitira, ndi kuti, "Inu ndi Mwana wa Mulungu, Mfumu ya Israeli." Kapena, inu mukhoza kunena kuti, "Hum. Iye ndi mdierekezi, wam'bwebwe, mtundu wina wa mzimu woyipa." Ndiye, zimenezo ziri pakati pa inu ndi Mulungu. Mukuona? Tsopano, tsopano, zimenezo ziri kwa inu, kuti muweruze Izo. Mukuona? Zimangotengera kawonedwe kanu kwa Izo.

358 Koma, kwa ine, ndi Yesu Khristu. Ndi, kwa ine, chifukwa lonjezo Lake. Ndipo tsopano ngati Iye anapanga lonjezo ndipo ananditumа ine, ndipo anandipatsa ine zizindikirozo . . .

359 Ndipo zaka zambiri zapitazo, ine ndinali kuno ndi anthu inu, ndipo Iye anandipatsa ine chizindikiro, ngati muyika dzanja lanu pa langa. Ndi angati akukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndiye ine ndimakhoza kukuuzani inu, ngati ine ndigwirabe kwa maminiti pang'ono. Ine sindimakhala ndi ulamuliro, koma kunena kuti inu muli ndi—chotupa kapena chirichonse chimene chinali. Izo zimakhala zangwiro. Nkulondola uko?

360 Ndipo ndinakuuzani inu, kuti Iye anandiuza ine, "Ngati ine ndikanati ndidzakhale wolemekeza ndi kukhulupirira, ndipo nkukhala mfulu," ndipo, ndipo zimenezo, osati kupita kumakapempha ndalama. Ndipo ine sindinayambe ndatengapo chopereka mmoyo wanga. Mukuona? Ndi chirichonse, "Ndi kukhala moona kwa Iye, kuti zidzafika pomadzachitika, kuti, pamene ndizidzamawauza anthu chinsinsi chomwe cha mtima wawo, chinthu china." Iwo samadzakana izo. Mukuona? Mukuona? Inu mukukumbukira ine ndikunenera zimenezo?

[Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Tsopano izo zachitika. Mukuona?

361 Tsopano, tsopano mungokhala molemekeza. Inu mukuti, “Kodi inu mukuyembekezera chiyani, M’bale Branham?” Pa Iye. Ine sindikumudziwa mkazi ameneyo. Ngati Iye sandidzoza ine, ine sinditha kuchita zimenezo. Ndizo zonse basi.

362 Ndi angati amene anayamba awonapo chithunzi cha Mngelo uja wa Ambuye, Moto uja, Lawi lamoto? Iwo anajambula Ilo, ali nacho konsekonse mdziko tsopano. Icho chiri ku Washington, DC, mu holo ya zaluso zauzimu. Chinthu chauzimu chokhacho chimene chinayamba chatsimikiziridwapo mwasayansi.

Ine ndingoyankhula nanu kwa miniti, kulumikizana.

363 Inde. Ambuye alemekezeke. Uh-huh. Ndi Izi apa. Uh-huh. Ine sindingathe kukuuzani inu momwe ine ndimadziwira izo, koma ine ndikudziwa Iye ali pomwe pano tsopano. Mukuona? Uko nkulondola. Izo ziri pomwe pano tsopano. Mathokozo akhale kwa Ambuye. Mukuona? Ndi Izi apa tsopano.

364 Inu muli ndi nthenda yapa khungu imene inu mukufuna kuti ine ndiyipempherere. Ngati izo ziri zoona, kwezani mmwamba dzanja lanu. Tsopano, kodi inu mukukhulupirira zimenezo ndi mtima wanu wonse?

365 Tsopano, inu mukhoza kunena kuti ine ndinalingalira zimenezo. Mukuona? Tsopano penyani ndipo muwone ngati ife tinalingalira zimenezo. Mukuona? Mukhale molemekeza kwenikweni. Iye akuwoneka kuti ndi munthu wabwino.

366 Tsopano, pakali pano ine sindingathe kukuuzani inu zomwe ine ndinakuuzani inu, poyamba. Tsopano, miniti yokha. Inde, nthenda yapa khungu, inu muli nayo. Mwakhala nayo kwa nthawi. Ngakhale munapempherereredwapo, chifukwa cha iyo. Ndiye, inu muli ndi chinachake cholakwika ndi mbali yanu. Uko nkulondola. Icho chinayamba chifukwa cha ngozi ya galimoto. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Tsopano inu mukukhulupirira, sichoncho inu? Mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, ine ndikupempha machiritso ake. Ameni. Pitani, mukukhulupirira.

367 Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ali yemweyo dzulo, Kuwala kwa kumadzulo kwa Mzimu Woyera?

368 Inu muli bwanji? Inu ndi ine ndife alendo kwa wina ndi mzake, nthawi yoyamba ya kukumana kwathu. Ngati ine ndikanati ndikuchizeni inu, ine ndikanatero. Ine ndikungoyimirira Mchiritsiyo, monga kazembe wotumidwa, kupempherera kutsimikizira Kwake. Koma ngati Mulungu ati andiuze ine chimene inu mwabwerera pano, inu mundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake, kapena wantchito Wake? Inu mukhulupirira zimenezo?

369 Chinthu chimodzi, pali mthunzi pozungulira inu, zikusonyeza kuti inu mukuvutika ndi vuto la manjenje, kusokonekera m'maganizo, vuto la manjenje. Zimakhala moyipa madzulo pamene dzuwa likuyamba kulowa. Uko nkulondola. Ndiye, chinthu china, inu muli ndi chotupa chimene inu mukudandaula nacho. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine pamene chotupacho chiri? Icho chiri pa bere lakumanja. Ndi choncho? Kodi inu mukukhulupirira tsopano? Tsopano, pali Chinachake pa ine, chikunena zimenezo, chikudziwa zimenezo. Nkulondola uko? Inu mukukhulupirira kuti Icho ndi Mulungu? Ndiye Yesu anati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira: ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira." Mulungu akudalitseni inu. Ameni.

Khalani ndi chikhulupiriro. Musakayikire. Mungokhulupirira ndi zonse zimene ziri mwa inu.

370 Mnyamata wamng'ono apo wavala tayi yamizeremizere, ungosiya kudandaula. Nyamakazi imeneyo ikusiya iwe, ngati iwe utangokhulupirira izo ndi mtima wako wonse. Mukuona? Iwe unali utakhala pamenepo, ukuyembekezera zimenezo, sichoncho iwe? Ndipo iwe ulibe khadi la pemphero. Iwe sukusowa limodzi. Ungokhulupirira izo.

371 Mwaona, chikhulupiriro chake chinakhudza Chinachake. Inu mukudziwa kuti mwamuna ameneyo sanandikhudze ine. Iye ali mapazi twente kutalikirana ndi ine. Nkulondola uko? Koma kodi iye anakhudza chiyani? Wansembe Wamkulu.

372 Ine ndinayang'ana apa kwa mkazi *uyu*, panali mwamuna. Ine ndinayang'ana, uyo anali mwamuna. Ine ndinati, "Izo sizingakhale. Pali . . . Uyo ndi mkazi." Ine ndinayang'ana, pali mwamuna. Ine ndinakuwona Kuwala kuja, kumene kwapachikika *apa*, kunapita ndi kukapachikika pafupi ndi iye. Ine ndinamuwona iye akuyesetsa kuti achoke pa bedi, monga choncho. Ndi zimenezotu. Mukuona? Ndi uyo pamenepo. Muloleni iye akhale umboni. Ndi choncho? Inu munali mutakhala, mukupempherera zimenezo. Nkulondola uko? Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse tsopano, ndipo inu mukhala bwino.

373 Kotero, "Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka." Mungokhala ndi chikhulupiriro. Tsopano khalani molemekeza kwenikweni.

374 Mundikhululukire ine. Ine ndimayang'ana Kuwalako, kukusuntha mozungulira, kudutsa mchipindachi. Ine—ine ndimangoyang'ana, mwaona.

375 Tsopano ine ndikufuna kuti ndiyankhule nanu mphindi chabe. Mukuwoneka ngati munthu wabwino, kwa ine. Ndife alendo kwa wina ndi mzake. [Mlongoyo akuti, "Inde, bwana."—Mkonzi]. Ambuye akudziwa mavuto anu. Iye

akundidziwa ine, akukudziwani inu. Ndife mwamuna ndi mkazi, tayima pano titakumana, nthawi yathu yoyamba. Ndi Mzimu, ndinu Mkhristu, ndipo—ndipo ine ndikutha kumverera kunjenjemera kumene kunali ndi mzimu wanu, inu mukudziwa, kumangosuntha. Ndipo ine ndikudziwa kuti inu simuli wongokweranawo. Inu ndi Mkhristu, inu mwaona. Kotero ndiye ndi zomwe ine ndikutanthauza, *wongokweranawo*, ndi wongolumpha kuchoka kumalo kupita kumalo, inu mukudziwa. Ndinu wobadwa mwatsopano, mwaona, ndinu Mkhristu weniweni. Ine ndikumverera kuti ndinu wolandiridwa, inu mwaona. Ndipo Mzimu Woyera pano ukulandira mzimu umenewo, chifukwa iwo ndi mzimu wapaubale. Mukuona? Ndife m'bale ndi mlongo. Inu simuli pano chifukwa cha inueni. Inu mukumuimirira winawake. Mzanu akuvutika ndi kupsyinjika kwa ziwanda. Inu mukukhulupirira zimenezo? [“Ine ndikudziwa.”] Mukayike mpango umenewo pa iye ndipo musakayikire, izo zikawasiya iwo. Mulungu akudalitseni inu.

Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Mungokhulupirira ndi mtima wanu wonse.

Inu muli bwanji, dona? Ndife alendo kwa wina ndi mzake.

376 Tsopano, winawake, penapake. Mulungu, zinali pati izo? Penapake mwa omvetsera, winawake, chinachake chachitika. “Inu mukudziwa bwanji izo, M'bale Branham?” Chabwino, ine ndikungodziwa izo. Mukuona? Mukuona? Izo ziri basi monga kungokoka moyo kuchokera mwa iwe, inu mwaona. Chinachake chinachitika. Winawake wachiritsidwa penapake. Ine sindikudziwa pamene izo zinali, koma mwinamwake Iye andiwonetsa ine kachiwiri.

377 Ndife alendo kwa wina ndi mzake, dona. Ine sindikukudziwa iwe, koma Mulungu akukudziwa iwe. Iwe uli pano kwa cholinga chinachake, mwinamwake kwa winawake, mwina zachuma, zapanyumba. Chirichonse chimene icho chiri, Mulungu akhoza kundiuza ine. Kodi iwe ukhulupirira izo? Iwe udziwa ngati izo ziri zoona. Zikupitirirabe kukhala wachinyamata akubwera pano, masomphenya akuwonekera a wachinyamata. Tsopano, iwe ukhulupirire ndi mtima wako wonse, ndipo Mulungu apereka izo. Mukuona? Ngati ine ndingakuuze iwe, iwe ukudziwa ngati ine sindikukudziwa iwe, izo zikuyenera kubwera kuchokera ku mphamvu ina ya chauzimu.

378 Ukukumbukira ulaliki wanga usikuuno, chimene ine ndimachikamba? [Mlongoyo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Tsopano, taonani. Mwinamwake, ngati ine ndingatero, monga Mngelo uja anatembenuzira nsana Wake. Tsopano, nanga bwanji ngati ine ndingatembenuzire nsana wanga, monga *chonchi*, kumene iwe uli. Mukuona? Chabwino. Tsopano, iwe basi—ungonena kwa Ambuye Yesu, “O Mulungu,” basi mu mtima mwako, “muwulule

kwa M'bale Branham chimene ine ndabwerera pano, kapena chinachake chokhudza ine," ndipo uwone ngati Iye angatero.

379 Inde. Ine ndikutha kumuwona mkaziyo pakali pano. Iye akuvutika ndi vuto la mmatumbo. Uko nkulondola. Ndi zophuka m'matumbo. Ndi zoona. Akazi a Cathan, inu mukhoza kupita kwanu tsopano ndi kukakhala bwino, ngati inu muti mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse. Pitani ndipo mukakhulupirire, pa njira yanu. Mukhulupirire izo.

380 Inu mukukhulupirira? Khalani ndi chikhulupiriro. Kodi inu mukuzindikira kuti Mulungu yemweyo amene analemba Baibulo akuyendayenda mu tchalitchi chaching'ono ichi chodzichepetsa pano usikuuno, mu msonkhano uno pano?

381 Tsopano, ndife alendo kwa wina ndi mzake, nafenso, bambo. Ine sindikukudziwani inu, sindinakuwonenipo inu mmoyo wanga. Ndife alendo angwiro. Tsopano, izo zikundifoola ine, anthunu. Ndi a . . .

382 Dona wakhala kumbuyo uko ali ndi kudzimbidwa, wakhala pachiwiri kuchokera kumbuyo, kumbali kumene kwa mzere umenewo apo. Munali inuyo, kanthawi kapitako, munali kuntunda kuno. Ngati inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, izo zikusiyani inu.

383 Nanga bwanji mwana ameneyo yemwe amadana ndi mafungo? Inu mukukhulupirira kuti Mulungu amuchiza iye? Ndi zimenezotu pamenepo. Ulemelero! Mdierekezi anazitaya zimenezo. Iye anatero. Mulungu akudalitseni inu, mlongo, m'bale. Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Ndizo zonse zimene inu mukuzisowa. Izo zimusiya mwanayo. Musaiwale.

384 Kodi iwo anakhudza chiyani? Kodi donayo anakhudza chiyani, chifukwa cha mwana wake? Ine sindikuwadziwa anthu amenewo, sindinayambe ndawawonapo iwo mmoyo wanga.

385 Ngati ife tiri alendo kwa wina ndi mzake, kwezani mmwamba manja anu pamenepo, anthunu, apo pamene izo ziri, uyo, dona, kwezani mmwamba dzanja lanu. Uko nkulondola.

386 Iye anali atayima pamenepo, akumupempherera mwana ameneyo. Ndipo Mzimu Woyera unapitirira kumayenda mmenemo, penapake. Ndipo ine ndinawona apo pamene izo zinali, ndipo ine ndinamuwona mwanayo ali—ndi vuto limenelo. Ndi uyo apo.

387 Mwanayo akhala bwino, mlongo. Musadandaule. Bwanji? Pali Kuwala kwenikweni mozungulira pamenepo tsopano. Ine ndikudziwa kuti Mulungu wayankha. Mukuona? Izo zimusiya mwanayo. Ine ndikudziwa kuti iye akhala bwino. Eya.

388 Izo zikungobwera paliponse, kuchokera kwa omvetsera tsopano. Ndizo, sungathe kuzitenga izo. Izo zangokhala paliponse. Mungochitira umboni Izo. Kodi inu simukukhulupirira mochuluka tsopano kuposa momwe inu

munakhulupirira kanthawi kapitako? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndithudi. Inu mukuona Izo ndi . . . Izo zikhoza kuchitika kwa aliyense wa inu ngati inu mutangokhulupirira izo. Mukuona? Mungokhulupirira izo.

389 Mundikhulukire ine, bambo. Ine—ine—ine sindina . . . Inu mukudziwa, ine sikuti ndabalalika. Koma ine basi . . . Ine ndimafooka kwenikweni. Ndipo ine basi . . .

390 Yesu, mkazi mmodzi anakhudza chovala Chake, ndipo Iye anati, "Ine ndazindikira kuti ukoma wachoka," ndiyo, mphamvu. Ndipo ngati Iye, Mwana wa Mulungu, nanga bwanji ine, wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo?

391 Tsopano, apa pali mwamuna. Mulole izo zichitike kwa munthu uyu. Ndiye nonse a inu mukhulupirira? Aliyense akumudziwa munthu uyu? Kodi aliyense akumudziwa munthuyu, kuzungulira kuno? Oh, inde, bwana. Chabwino. Tsopano, inu mukudziwa. Tiyeni tiwone ngati Izo ziri zoona kapena ayi. Bamboyu ndi mlendo kwathunthu. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye mmoyo wanga.

392 Ndife alendo kwathunthu kwa wina ndi mzake. Koma Mzimu Woyera ukhoza kuwulula kwa ine chimene inu mwabwerera pano, kapena chimene inu mukufuna, kapena chinachake chokhudza inu, chimene inu mukuchidziwa, chimene ine ndikudziwa kuti sindikudziwa kalikonse, ndiye izo zingakukhutitseni inu kuti izo zikuyenera kukhala Mzimu Woyera.

393 Kodi izo zingakhutitse nonsenu, ndi kudziwa kuti Mzimu Woyera womwewo umene uli pano uli kunja uko, nawonso, mwa ife tonse?

394 Vuto lanu ndi vuto la thumbo. Ndi chotupa mu thumbo. Pali winawakenso pano akupemphera za zimenezo, ndi mkazi wanu kunja uko. Iye akumakhala ndi kupweteka kwa mutu kosasiya, nthawi zonse. Uko nkulondola. Inu muli ndi mwana kumeneko, nanunso. Uko nkulondola. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiwuza ine chimene chamuvuta mwana ameneyo? [M'baleyo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Ndi vuto la magazi. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine yemwe inu muli? ["Inde."] Kodi inu mungandikhulupirire ine? Inu ndi mtumiki. ["Inde."] Ndinu M'busa Bambo Mann. ["Inde."] Pitani kwanu, mukakhale bwino.

395 Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Mungomupatsa Mulungu matamando.

396 Kodi inu mukukhulupirira, dona, ndi mtima wanu wonse, mwakhala apo? Kodi inu mukukhulupirira? Pitani, mukadye nkhomaliro yanu. Vuto lanu la mmimba likusiyani inu, ndipo inu mukhala bwino.

397 Vuto lanu la nsana lachokanso, mlongo, kotero inu mukhoza kungopita kudutsa mchipindacho, ndipo mukhulupirire ndi mtima wanu wonse kuti Mulungu akuchiritsani inu. Inu mukukhulupirira zimenezo? [Mlongoyo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Muzingopita, mukufuula, ndi kuti, "Ambuye alemekezeke!" Chabwino, ndi mtima wanu wonse.

398 Manjenje ndi chinthu choyipa, koma Mulungu akhoza kuwachiza iwo. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Muzingopita, mukusangalala, mukuti, "Zikomo Inu, Ambuye." Mulungu azipanga izo kukhala bwino.

399 Mimba yakale imakuvutitsani inu? Pitani, mukadye, Yesu Khristu wakuchizani inu. Khalani ndi chikhulupiriro.

Nsana wanu ukukuvutitsani inu. Sichoncho iwo? [Munthuyo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Pitani, mukhulupirire. Yesu Khristu wakuchizani inu. Mukhale ndi chikhulupiriro.

400 Manjenje? Mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? [Munthuyo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Pitani, muchiritsidwe mu Dzina la Yesu.

401 Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Kodi Yesu Khristu sali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse?

402 Tsopano, Yesu anati, "Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita nayenso adzazichita." Nkulondola uko? Tsopano, kodi Yesu ananena izi: "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira"? Ndi okhulupirira angati ali pano? Chabwino.

403 Ndi angati akufuna kuti achiritsidwe? Kwezani manja anu. Ndiye ikani manja anu pa wina ndi mzake. Ndinu okhulupirira. Uko nkulondola. Iye amasunga Mawu Ake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ngati inu muti mukhulupirire izo, inu muwona chinachake chikuchitika chimene inu simunayambe mwachiwonapo kale, ngati inu muti mukhulupirire izo.

404 Tsopano weramitsani mitu yanu. Ikani… Musadzipempherere nokha, mumupempherere munthu amene inu mwayikapo manja anu. Pempherani tsopano, moonamtima. Mukhulupirire, moonamtima. Ikani manja anu pa winawake ndipo mumupemphere. Tsopano ine ndipemphera, apa.

405 Atate Akumwamba, ife tikubwera mu Dzina la Ambuye Yesu. Ife tikubwera chifukwa chakuti Mawu Anu atsimikiziridwa. Kutumidwako kwatsimikiziridwa. Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, ali mu kukhalapo kwathu, m'mawonekedwe a Mzimu Woyera. O Mulungu, awa ndi anthu Anu. Iwo akuvutika. Satana wawamanga iwo. Iwo akudziwa kuti Inu muli pano. Kutsimikizira kwa Kukhalapo Kwanu kuli pano, Yesu Khristu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

406 Satana, iwe walephera nkhondoyo. Tuluka mwa iwo, Satana, mu Dzina la Yesu Khristu. Ine ndikukulamulira iwe kuti uwasiye omvetsera awa ndipo utuluke mwa anthu awa, kuti iwo akhoze kupangidwa amfulu, mu Dzina la Yesu Khristu.

407 Ngati inu mukukhulupirira izo, imani pa mapazi anu ndipo mumupatse Mulungu matamando. Ndiro lingalirolo. Ndi zimenezotu. Kwezani manja anu ndipo mupatseni Iye matamando. Kutsimikiziridwa! Muvomereze ndipo mukhulupirire kuti machiritso anu abwera.

62-0122 Kutsimikizira Kwa Kutumidwa
Assembly Of God
Tempe, Arizona U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org